# *Chifukwa Chimene*

# *Ankayenera Kukhala M'busa*

. . .Ine ndikuganiza, wokhala ngati mlaliki wotalikitsa. Ndipo wopanda maphunziro, ine—ine ndikuganiza sindimamveka ngati mlaliki kwa anthu ena. Ndipo ine—ine sindimadzinenera nkomwe kuti ndine mlaliki, ndimangokhala ngati theyala lothandizira. Koma ine ndikumverera kuti ine ndiri ndi Uthenga wochokera kwa Mulungu, kuti mwanjira yanga (kuti njira yokhayo imene ndikuyenera kuwuperekera Iwo), ine ndikuyesetsa kuti ndiwupereke Iwo kwa dziko lapansi. Ndipo ngati sindingakhale ndi Uthenga umenewo, ndingakhale womupachika Mulungu ndi wachinyengo kwa inu. Munthu amene anganene chinthu chimodzi ndi kukhulupirira china, ndi wachinyengo. Ife nthawizonse tidziyesetsa kuyankhula choonadi kuchokera mu mtima mwathu. Kuti pamene anthu ayang'ana pa ife, ngakhale iwo akutsutsana nafe ife, tikufuna tidzikhala amuna ndi akazi olemekezeka: kuti timayankhula kuchokera pansi pa mtima wathu, icho chimene chiri choona mmitima mwathu.

2 Chaka chatha, kapena chaka chinacho, ndinali ndi mwayi woyankhula a—Mkhristu. . .kapena pepani, uthenga wa Khrisimasi, kuno ku Ramada. Ndipo ine ndikukhulupirira ine ndinayankhula pa phunziro, mwina kuno kapena ku Phoenix, la: *Chifukwa Chiyani Betelehemu Wamng'ono*? Ndipo ine ndikukhulupirira ndiye kunali kuno, chaka chatha, ndinayankhula pa: *Ife Taiwona Nyenyezi Yake Kummawa Ndipo Tabwera Kuti Tidzamupembedze Iye*.

3 Ndipo, inu mukudziwa, timawerenga Baibulo, ndipo timadabwa, ma *"Chifukwa chiyaniwo*?" Ndipo usikuuno ine ndimaganiza, ngati inu mungapirire nane kwa kanthawi, ndi kupemphera nane, ine ndingayesere kuti ndikupatseni inu uthenga wanga wa Khrisimasi. Mulungu yekha ndi amene akudziwa kumene ife tidzakakhale Khrisimasi yotsatira, ngati idzakhalepo Khrisimasi yotsatira ikatha iyi. Chotero pokhala kuti iyi ikhoza kukhala Khrisimasi yomaliza ife takhala pamodzi, mpaka titadzakhala pa tebulo lina. Ndipo Iyo siidzakhala ina ya mtundu uwu, koma idzakhala pamene ife tizidzadya ndi kumwa mgonero mwatsopano ndi Iye, mu Ufumu wa Atate kumapeto kwa ulendo. Ndipo potero, tiyeni tiyandikire iwo usikuuno ngati kuti uwu ndi uthenga womaliza wa Khrisimasi umene ife tidzakhale konse limodzi, mu kuya kwa kuwona mtima.

4 Ine ndikufuna kuti ndiyankhule usikuuno pa phunziro lachilendo, koma nthawizina mumamupeza Mulungu mu chinthu chachilendo. Iye amachita zinthu mwanjira yachilendo. Osati njira yachizolowezi, ndi njira yosazolowereka, nthawi zosazolowereka, zochitika zosazolowereka, Iye ndi wosazolowereka. Ndipo ndikufuna ichi . . . Ambuye akalola, ndikufuna kuti ndiyankhule pa mutu wa: *Chifukwa Chimene Ankayenera Kukhala M'busa*.

5 Ndipo tsopano ife tisanayandikire Mawu, amene ine ndikukhulupirira kuti amenewo ndi Mulungu, "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anadzasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu."

6 Monga ndinanenera, sabata yapitayi, kapena sabata inayo ku Phoenix, "Zatsimikiziridwa kuti alipo anthu a dziko lapansi lino, anthu, akudutsa mchipinda chino panopa." Televizioni imatsimikizira zimenezo. Ali mu dera lina, maso athu achirengedwe ndi zokhudzira zathu zisanu sizingathe kuzitola izo. Sikuti televizioni imapanga chirichonse, imangowulutsa chabe. Inu simungakhoze kusuntha ndi chala chanu, simungakhoze kuphethira diso lanu, koma zinatsimikiziridwa kuti zimajambulidwa kwanthawizonse. Ine ndikhoza kuyimirira . . . Kapena mwamuna ku Australia, akhoza kukhala ndi—televizioni apa, osati zokhazo koma—mwamunayo akhoza kuyankhula, kusuntha chala chake, kuphethira diso lake, kapena ngakhale mtundu wa zovala zimene iye wavala, zikhoza kuwonetsedwa kuno pa khoma; ndipo iye ali mu Afrika, Australia, kuzungulira dziko. Mwaona, ulipo mkombero wa mafunde a ifara. Ine sindingathe kuzifotokoza izo, koma ine ndikudziwa ziripo kumeneko. Ine sindikuganiza kuti aliyense angazifotokoze izo kwenikweni. Chotero, televizioni imatha kuzikoka izi ndi kuzipanga izo kukhala chenicheni ndi zida zina, zimene iwo akhoza kuziwonetsa izo pa khoma.

7 Tsopano, chinthu chomwecho chinali kuno pamene Adamu anali kuno. Televizioni inali kuno pamene—pamene Eliya anakhala pa Phiri la Karimeli. Kunali kuno pamene Martin Luther, wansembe wamng'ono uja, anatayira mgonero pansi ndikuti, "Ndi mkate! Ndipo olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro." Zinali kuno ndiye, koma ife tikungozipeza kumene izo pano. Ndipo izo zirinso chomwecho, kuti mu kupezeka kwathu usikuuno alipo Mulungu, Angelo, zamoyo zauzimu zimene nzosawoneka kwa chokhudzira chathu chachirengedwe cha kupenya. Koma tsiku lina zidzakhala zenizeni chimodzimodzi basi monga momwe televizioni iliri tsopano, ndipo basi zawamba. Tsopano, icho ndi chifukwa chake ine ndimakhulupirira Mawu.

8 Yesu anati, "Aliyense amene adzawonjezera mawu amodzi ku Baibulo ili, kapena kudzachotsa Mawu amodzi kwa Ilo, gawo

lake lidzachotsedwa mu Bukhu la Moyo."

9 Chotero, tiyeni ife tiweramitse mitu yathu ndiye, ife tisanawerenge nkomwe Ilo. Molemekezeka kwambiri! Munthu aliyense amene ali ndi mphamvu yakuthupi akhoza kutsegula tsamba, koma ndi Mulungu yekha angawawulule Iwo.

10 Ndipo ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano ku fumbi kumene tinatengedwako, ndipo tsiku lina tidzabwererako, ine ndikudabwa. . .Ndipo munthawi yopatulika iyi, pamene tikuyandikira Khrisimasi, ngati pali ena pano amene akumverera kuti ndi osayenera ndipo akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero ili, inu mungatero (popanda kutukula mutu wanu) mungokweza manja anu kwa Mulungu ndi kuti, "Ndikumbukireni ine, Ambuye, Khrisimasi ino"? Mulungu akudalitseni inu.

11 Atate Oyera ndi Achifundo Akumwamba, Mulungu Wamphamvuzonse, Iye amene analiko kuchokera pachiyambi, kusanakhale nyenyezi, kapena atomu, kapena molekyu. Inu munapanga zinthu zonse kudzera mwa Yesu Khristu Mwana Wanu, ndipo mwatipatsa ife zinthu zonse mwaulere mwa Iye. Ife tikukuthokozani Inu, usikuuno, Ambuye, chifukwa cha mwayi uwu umene Inu mwatipatsa ife kuti tisonkhane pamodzi, kuti tidzachenjezedwe ndi kuphunzitsidwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo Mzimu Woyera umatenga Mawu Anu ndi kuwaululula Iwo kwa ife, pakuti Yesu anati, "Pamene Iye Mzimu wa Choonadi adzabwera, Iye adzakukumbutsani inu zinthu izi zimene ndanena komanso adzakuwonetsani inu zinthu zimene ziri nkudza."

12 Mulungu, palibe mmodzi pakati pathu, ndipo palibe wina padziko lapansi, amene ali woyenera kuyesa kutanthauzira Mawu Anu, pakuti kunalembedwa kuti, "Mawu a Mulungu alibe kutanthauzira kwa mseri." Chotero, Ambuye, tikupemphera kuti Mzimu Woyera utipatse ife usikuuno, wina aliyense, gawo limene tikulifuna kuti likhutitse njala imeneyo imene ili mu mtima mwathu yoyenda pafupi ndi Inu. Ife ndi osakwanira, odetsedwa, osayenera. Mulole Mwana amene anabadwira mu Betelehemu, amene anakhala moyo wangwiro kwambiri, ndipo anali munthu wangwiro yekhayo padziko lapansi, ndipo anadzipereka Yekha dipo kuti Iye akakhoze kutitsuka ife ochimwa odetsedwa ndi kutibweretsa ife mu ubale ndi Atate, perekani usikuuno kuti Mzimu Wake Woyera (kudzera mu kulalikira kwa Mawu) utichitire ife zimenezo.

13 Ambuye Mulungu, alipo odwala ambiri mu dziko lero, pamaso pa mankhwala apamwamba kwambiri amene ife tinayamba tasamalidwapo nawo, ndi mankhwala apamwamba ndi zipatala zapamwamba. Ndipo komabe muzofufuza zathu zazikulu zonse za sayansi, komabe pali matenda ambiri kuposa omwe dziko lapansi linayamba lawadziwapo, chifukwa pali

uchimo wochuluka ndi kusakhulupirira kuposa momwe dziko linayamba ladziwapo. Tithandizeni ife usikuuno, Msing'anga Wamkulu, ndipo mudzachiritse odwala amene ali pakati pathu.

14 Ndipo mutipatse ife Mzimu, Mzimu woona wa Khrisimasi. Pamene lero. . .kuti pamene miyambo yachikunja, mitengo ya Khrisimasi ikupembedzedwa, nkhani zopeka za a— munthu wotchedwa Santa Claus, ndi za akalulu athu a Isitala, ndi mafashoni osiyanasiyana amene dziko lamalonda lakhazikikapo, mulole izo ziyikidwe pambali, Mulungu. Mutilole ife tikalowe mwa Khristu Mawu, pakuti tikupempha izi mu Dzina Lake ndi kwa ulemelero Wake. Ameni.

15 Ngati mungatembenuzire ndi ine kuti tiwerenge mu Malemba Oyera, Luka Woyera, mutu wa 2. Kodi mukukhoza kundimva ine bwinobwino?

Kodi pali kusintha kulikonse pa maikrofoni? Kodi mukukhoza kundimva ine kumbuyoko bwinobwino? Ngati mukutero, kwezani dzanja lanu. Zikomo inu. Mutu wa 2 wa Uthenga molingana ndi Luka Woyera.

> *Ndipo zinachitika mmasiku amenewo, kuti panatuluka lamulo lochokera kwa Kaisara Augusto, kuti dziko lonse likalembetse.*
>
> *(Ndipo* kalembera *uyu* anadziwitsidwa *koyamba. . . anali kazembe wa Siriya.)*
>
> *Ndipo onse anapita kukalembetsa, aliyense* ku dziko *lakwawo.*
>
> *Ndipo Yosefe anapita kumtunda kuchokera ku Galileya,* kupita *ku mzinda wa Nazareti, ku Yudeya, . . . mzinda wa Davide, umene umatchedwa Betelehemu; (chifukwa iye anali wa mnyumba ndi mzere wa Davide)*
>
> *Kuti akalembetse ndi Maria mkazi wopalidwa naye ubwenzi, ali woyembekezera kwambiri.*
>
> *Ndipo chotero kunali, kuti, pamene* iye anali *kumeneko, masiku* a kukwaniritsidwa kwake *kuti iye abereke.*
>
> *Ndipo anabala mwana wake wamwamuna woyamba, ndipo anamukulunga iye mu zovala zapagoli, ndipo anamuyika iye mu chodyera ng'ombe; chifukwa panalibe malo awo ku nyumba ya alendo.*
>
> *Ndipo pamenepo* panali *abusa mu dziko lomwelo akukhala* mminda, *akuyang'anira* ziweto *zawo usiku.*
>
> *Ndipo, taonani, mngelo wa Ambuye anadza pa iwo, ndipo ulemelero wa Ambuye unawala* mowazungulira *iwo: ndipo iwo anali ndi mantha aakulu.*
>
> *Ndipo mngelo anati kwa iwo, Musaope ayi: pakuti, taonani, ine ndabweretsa. . .uthenga wabwino wa*

*chimwemwe chachikulu, umene udzakhala kwa anthu onse.*

*Pakuti kwa inu kwabadwa lero mu mzinda wa Davide Mpulumutsi, amene ali Khristu Ambuye.*

*Ndipo ichi chidzakhala chizindikiro kwa inu;* Inu *mukamupeza mwanayo atakutidwa ndi nsalu yapagoli,* atagona *mu khola.*

*Ndipo mwadzidzidzi panali* a. . .*Ndipo mwadzidzidzi pamenepo*. . .*ndi mngelo khamu la*. . .*khamu lakumwamba likutamanda Mulungu, ndi kunena,*

*Ulemelero ukhale kwa Mulungu wa mmwambamwamba, ndi mtendere pansi pano, mafuno abwino kwa anthu.*

*Ndipo kunadzachitika, pamene angelo anachoka kwa iwo kupita kumwamba, abusawo ananena wina ndi mzake, Tiyeni tipite tsopano ku Betelehemu, ndipo tikawone chinthu ichi chimene chachitika, chimene Ambuye* wa*tidziwitsa ife.*

*Ndipo iwo anapita* mwa*changu, ndipo anakamupeza Mariya, ndi Yosefe, ndi khandalo litagona mu khola.*

*Ndipo pamene iwo anamuwona iye, anadziwitsa anthu za mawu amene anayankhulidwa kwa iwo okhudza* za *mwanayo.*

*Ndipo iwo onse amene anamva anadabwa ndi zinthu zimene iwo anauzidwa ndi abusawo.*

*Koma Mariya anasunga zinthu zonsezi, ndipo anaziganizira izo mumtima mwake.*

*Ndipo abusawo anabwerera, akulemekeza ndi kutamanda Mulungu chifukwa cha zinthu zonse* zimene *iwo anazimva ndi kuziwona, monga izo zinanenedwa kwa iwo.*

Ambuye awonjezere madalitso Ake ku kuwerenga kwa Mawu Ake.

16 Tsopano, ndi. . .Chifukwa chiyani chochitika chachikulu ichi chinaululidwa kwa azibusa? Icho chingakhale chinthu chodabwitsa kwa ife. Ine ndiri ndi Malemba ena ndawalemba apa, ndi zolemba zingapo zimene ine nditi ndiyesere kuti ndidutsemo, kuti ndikufotokozereni inu *chifukwa chiyani* mwakudziwa kwanga kopambana. Ndipo mwinamwake ndiye zitatha izi, kuti Ambuye ndi chisomo Chake, usikuuno, achotsa ma *chifukwa chiyani* kwa ife. Koma anatero. . .Pafupifupi onse a ife, ine ndikuganiza, pa nthawi ina kapena imzake, takhala tikudabwa chifukwa chiyani chochitika chachikulu ichi cha nthawi zonse chinaululidwa kwa azibusa. Nchifukwa chiyani Icho chinaululidwa kwa azibusa ndipo osati kwa

afioloje a tsiku limenelo? Iwo anali amene anaphunzitsidwa kuti adzachimve Icho. Ndipo nchifukwa chiyani Icho chinabwera ndi kudzawalambalala olemera, ndi kubwera kwa osauka? Komanso, nchifukwa chiyani Icho chinawalambalala ophunzira ndi anzeru, ndi kubwera kwa odzichepetsa ndi osaphunzira? Pali mafunso angapo a *chifukwa chiyani* mu izi.

17 Ndipo chifukwa china chimene ine ndinganene, zindikirani, mwanayo anabadwira mu Betelehemu. Chimene Betelehemu mu kutanthauzira kwa Chihebri, monga ife tinali nazo zaka zingapo zapitazo kuno, *Betelehemu* amatanthauza "nyumba ya mkate wa Mulungu." Ndipo ife tinatsimikizira mu Malemba, Iye sakanabwera ku malo ena aliwonse. Betelehemu anakhazikitsidwa ndi Rahabu ndi wake—mwamuna wake. Rahabu anali hule amene mkulu wa asirikali ankachita naye chibwenzi, kuchokera ku—gulu la nkhondo la Israeli, iwo atatha kulanda Yeriko. Ndipo mwa chikhulupiriro iye anakhulupirira Uthenga wa Mulungu, mu chikhalidwe chakecho, ndipo iye anapulumutsidwa. Ndipo kuchokera pamenepo, pamene Yoswa anagawa malo a kumene aliyense akanadzakhala, . . .

18 Ndipo pamenepo pali phunziro lalikulu limene nthawiyina ine ndikuyembekeza kuti ndidzatha kulibweretsa ku Tucson, la azimayi a Chihebri amenewo akamabereka ana amenewo. Pamene iye ankabuula pa ululu wakubala wa mwanayo, iye ankamutcha dzina mwanayo ndipo izo zinkamuika iye pamalo mdziko lolonjezedwa, fuko lake. Chinthu chachikulu, Mawu onse a Mulungu amalumikizana pamodzi. Ngati iwo sakulumikizana pamodzi, si Mawu a Mulungu amene sakulumikizikawo, ndi ganizo lanu limene silikulumikizika kwa Mawu. Iwo onse amagwirizana pamodzi.

19 Chotero, ndiye, Iye anali Mkate wa Moyo, monga ife tinaphunzitsira sabata yatha ku Phoenix, kapena sabata inayo. Ndipo pokhala Mkate wa Moyo, Iye sakanakhoza kubwera kwina kulikonse koma ku "*nyumba ya mkate wa Mulungu*." Ndipo icho chinali *chifukwa chiyani*. Tsopano, apa, Yesu anabadwira ku Betelehemu, ndipo ku Betelehemu kunali sunagoge, atsogoleri aakulu achipembedzo ankakhala ku Betelehemu. Davide mfumu-m'busa wamkulu anabadwira ku Betelehemu, abambo ake a Jesse anabadwira ku Betelehemu, agogo ake Obedi anabadwira ku Betelehemu. Komanso, njira yonse kubwerera, iye anachokera ku Betelehemu.

20 Ndipo apa, Yesu Mwana wa Davide anabadwira ku Betelehemu, pansi pa mithunzi ya chitchalitchi chachikuluchi. Ndiye ngati anthu amenewo anali ophunzitsidwa, ndipo anakhala akumuyembekezera Mesiya kwa zaka zonsezi; zaka foro sauzande, Mesiya anali ataneneredwa kuti adzabwera. Ndiyeno ngati Mesiya adzabadwire mu mthunzi wa chitchalitchi, nchifukwa chiyani iwo anachita kupita kumbuyo uko kukwera mmapiri kwa gulu la abusa

osaphunzira, osaphunzitsidwa kuti akabweretse Uthenga waukulu, Uthenga woyamba? Ndipo anawatuma azibusa! Osati anzeru ndi ophunzitsidwa, koma azibusa. Ndi chinthu chachilendo, sichoncho izo? Koma pakuyenera kukhala *chifukwa* penapake. . .Apo pali *chifukwa,* tsopano pakuyenera kukhala yankho la chifukwa chiyani! Ndipo palibe munthu amene akudziwa yankho kupatula Mulungu. Iye ndi Amene akudziwa yankho lake.

21 Tsopano, kumbukirani, Mesiya anali alikale mu mzindawo, atabadwira mu mzindawo, mu khola; pomwepo pafupi ndi matchalitchi aakulu kumene wansembe wamkulu. . .ndi ansembe aakulu, ndi afioloje, ndi anzeru, ndi ophunzitsidwa, onse anali kumeneko akumudikirira Mesiya. Ndipo apo Iye anali, pakati pawo pomwe! Koma nchifukwa chiyani ndiye iwo anapita ku. . .anapita ku mapiri a Yudeya kwa osaphunzira, osaphunzitsidwa, opanda khalidwe, osaukitsitsa mwa onse? Amawoneka ngati munthu wosayenera kwambiri pa ntchito yoteroyo, kuti awawululire Uthenga ndi kuwatuma iwo kuti akabweretse Uthenga.

22 Inu mukudziwa lingaliro langa? Ilo silingakhale lopindula kwambiri, koma ndikufuna ndipereke lingaliro langa: Ine ndikukhulupirira ndi chifukwa cha nzeru za Mulungu, kuti Iye ankadziwa kuti iwo sakanalandira Uthenga woterowo momwe Iwo unabwerera. Izo sizinali mwa mamvedwe a kuphunzira kwawo. Izo zinali zosiyana. Izi sizinali zimene iwo anaphunzitsidwa kukhulupirira kuti Iye akanadzakhala. Izo zinali zosiyana ndi kumvetsetsa kwawo kwa fioloje. Maphunziro awo onse, kuphunzira kwawo konse kunalambalalidwa, kunasanduka kopanda pake. Ine ndikukhulupirira kuti inali nzeru ya Mulungu imene inadziwa kuti iwo sakanadzalandira Uthenga woterowo.

23 Chotero Mesiya anali kuno, ndipo pamayenera kudzakhala winawake woti adzazindikire Izo. Ndipo Iye ankawadziwa iwo amene anali asanasokonezeke ndi zinthu ngati zimenezo. Iye akanadzakhala wokhoza kupititsa uthenga Wake kwa gulu losaphunzira, kuposa momwe Iye akanachitira kwa gulu losokonezeka limene linali litakhazikika kwambiri mu njira zawo limene panalibe kanthu komwe kakanawatembenuza iwo, osati ngakhale Mawu a Mulungu.

24 Ndipo tsopano, mzanga wa Chikhristu, undilole ine ndikufunse funso ili, ndi kuwona mtima konse ndi chikondi. Ine ndikungodabwa ngati Iye angachite kachitidwe komweko usikuuno, ndi kutumiza kwa ife mu kam'badwo kano Mawu olonjezedwa amene analonjezedwa kwa kam'badwo kano, ine ndikudabwa ngati azafioloje athu, ndi ophunzitsa, ndi anzeru, sangawukane Uthenga chimodzimodzi monga momwe iwo anachitira nthawi imeneyo? Munthu samasintha, ngakhale

Mawu a Mulungu samasinthanso. Iye ndi Mulungu wosasintha, Iye samasintha!

25 Zindikirani, Angelo akubwera ndipo. . .Angelo akubwera ndi kudzapereka Uthenga wawo kwa anthu otsika chonchi, pamene kunali anthu kumeneko ochuluka (oganiziridwa padziko lapansi) oyenerera kuposa azibusa osauka awa, osaphunzira. M'busayo anali wosaphunzira kwambiri kuposa wina aliyense, iye sankasowekera kudziwa kalikonse koma za nkhosa zake zokha. Iye sankasowa kuti adziwe masamu. Iye sankasowa kuti adziwe momwe—angaigawire atomu. Iye sankasowa maphunziro aliwonse. Iye ankangoyenera kudziwa nkhosa zake, ndizo zonse zimene iye ankayenera kuti azidziwe. Ndipo Mulungu, Wanzeru zazikulu, ndi Kasupe ndi gwero la nzeru zonse, angasankhe munthu ngati ameneyo (anthu, kani, monga amenewo), ndi kuwalambalala ma sikolala onse ophunzitsidwa bwino amene anaphunzitsidwa kudziwa Zimenezo. Icho chimayankhula chinthu chimodzi, kuti iwo anaphunzitsidwa ntchito yolakwika. Kuwalambalala ofunikira onse apa dzikolo; panali anthu ofunikira, aphunzitsi apamwamba, Kayafa mkulu wa ansembe, amuna ena aakulu opambana, ophunzira apamwamba onse aku Israeli, zipembedzo zonse, ndi afioloje onse odzitamandira, Mulungu anawalambalala onse a iwo! Tsopano, imeneyo ndi nzeru ya Mulungu.

26 Zindikirani, Miyamba Yammwamba ikufulumira kudzalemekeza odzichepetsa kwambiri ndi osaphunzira. Mmwamba mwa Kumwamba munatsika kudzazizindikiritsa Yekha kwa otsikitsitsa apa dziko lapansi, kuwalambalala onse apakati kuti adzazidziwitse Yekha kwa olishya awamba; kubwera kudzawapatsa olishya awamba awa Uthenga waukulu kwambiri wa nthawi zonse. Pakhala pali amithenga ambiri opambana. Ife tikhoza kuganiza za mmasiku a Nowa, ndi aneneri, ndi—ndi ansembe aakulu, ndi ena otero, analipo mmasiku apitawo. Munthu wophunzira kwambiri, mafumu, amphamvu, mafumu, koma apa Iye akubwera ndi wopambana wa Mauthenga onse. Uthengawo unali chiyani? "Mesiya ali pano tsopano!" Mukuona? Ndipo kuti izo zidziwike, Iye anawadutsa onse ophunzitsidwa, kuti adzazidziwitse izo kwa azibusa odzichepetsa.

27 Taganizani za zimenezo: mwa akulu ampingo onse, amuna onse a mpingo, aphunzitsi onse, onse a—maphunziro afioloje, ndalama zonse zinawonongedwa, mipingo yonse, ndipo ziphunzitso, ndi zipembedzo, zonse zinalambalalidwa! Kuphunzira konse kumene iwo anali nako pa—mamishonare onse, ndi kutembenuza anthu konse, umembala wonse, ndi zonse zimene iwo ankaganiza kuti ankachita ulemu kwa Mulungu, komabe Uthenga wofunikira wa zonse za zimenezo unalambalalidwa kwa iwo. Zachilendo! Chifukwa chiyani?

Mukuona?

28 Ndipo zindikirani, osati zokhazo, koma malo osayembekezeka kwambiri a chochitika choterocho. Azibusa, tsopano, anali iwo amene analandira Uthenga. Ndipo tsopano zindikirani kumene Uthengawo unakafikira: ku malo osayembekezereka kwambiri amene aliyense angayembekezere kuti Iwo ungabwereko. Ndipo ine ndikudabwa, usikuuno, ngati tikufunafuna Uthenga woona wa Ambuye Yesu, ndikudabwa ngati Iwo ukanakhala mu gulu losayembekezeka, malo amene anali. . .amene dziko lalikulu, lotukuka kwambiri ndi mpingo lero lingaganize kuti linali gulu la—la, oh, ampatuko? Ine ndikudabwa ngati uko sikukanakhala kumene ife tikanakamupeza Iye? Malo osayembekezeka kwambiri, ndiponso kwa oyankhula osayenera. Azibusa samadziwa kalikonse za kuyankhula, kuziyitana nkhosa basi; chabwino, mwinamwake ndi chifukwa Iwo unabwerako.

29 Koma panali Mawu olonjezedwa. Zindikirani, izo zikhoza kuchita izo kachiwiri.

30 Iwo unawalambalala anthu onse apamwamba a mdzikolo. Iwo unawalambalala apamwamba onse, ndipo unawululidwa kwa osadziwika. Apamwamba onse amene anakongoletsedwa ndi—ndi udokotala waumulungu waukulu ndi—ndi zowerenga maganizo, ndi—ndi maphunziro apamwamba, ndi zimatchalitchi zazikulu ndi zinthu, izo zonse zinalambalalidwa ndipo unawululidwa kwa osadziwika. Nzeru, nzeru zopanda malire za Mulungu Wamphamvuzonse zinachita zimenezo, kuwadziwitsa iwo Uthenga waukulu umene unayamba wakhalapo, "Mesiya tsopano ali pa dziko lapansi." Nzeru yakeyo! Zikanabwera kokha kuchokera kwa Mulungu amene amadziwa nzeru! Nzeru zonse ndi kuphunzira konse, ndi chirichonse, tsopano zinasiidwa kuti ziwonongedwe ndipo zinalambalalidwa ndi nzeru zazikulu za Mulungu. Ine ndikumangobwereza zimenezo chifukwa ndikufuna kuti zipite pansi penipeni. Zonse zinawonongedwa, izo sizinali zabwino. Anazilambalala zonsezo kuti akalole nzeru ya Mulungu ikakhale ndi njira yoyenera, kuti Mulungu amatenga zopanda pake kuti akazipange kukhala zinthuzinthu.

31 Ife tikhoza kuyimira apa ndi kuyankhula za Yohane. Ife tikhoza kuyimikira ndi kuyankhula za Eliya. Palibe amene amadziwa kumene Eliya anachokerako. Zonse zimene iwo amadziwa, iye anangowonekera pa chochitikacho. Aneneri mmbuyomo kudutsa mu mibadwo, iwo anali osadziwika. Koma Mulungu anazitenga zimenezo ku. . .ndipo analambalala a—ndondomeko za mpingo, ndi ziphunzitso, kuti akapange. . . akawonetsere kuti Iye ndi Mulungu. Iye amatenga chinachake chimene sichiri kanthu, kuti akachite chinachake ndi icho. Iye amasonyeza nzeru Zake ndi Umulungu Wake pochita chomwecho, kuti Iye amatenga osadziwika. Pamene Iye anamupanga munthu poyamba, Iye anangotenga mpira wa

dongo ndipo anamupanga munthu kuchokera kwa ilo. Pamene panalibepo kanthu koma dongo, koma Iye anamupanga munthu. Ndipo Mulungu amatenga zosadziwika tsopano, kuti achite nazo zinazake. Ndipo nthawizonse pamene ife tiganiza kuti ndife zinthu zinazake, ndiye sitingagwiritsidwe ntchito mdzanja la Mulungu. Ife tikuyenera kusiya zonse zimene tinayamba tazidziwapo kapena kuphunzira. [M'bale Branham akukonza kummero kwake—Mkonzi]. (Mundikhulululukire ine.) Monga Paulo Woyera wamkulu, iye anati amayenera kuyiwala zonse zimene anaphunzira, kuti amudziwe Khristu.

32 Kuphunzira kwawo konse, ziphunzitso zawo zonse ndi zina zotero, zinkagwira ntchito mowayipira iwo. Pomaliza izo zinamukana Iye! Kuphunzira kumene iwo anali nako *kwa* Iye, kuti amukhulupirire Iye, anatembenuka ndipo anadzakhala mdani Wake wotsutsa kwambiri, ndipo anamupachika Iye!

33 Kodi inu mukudziwa kuti mbiriyakale imadzibwereza yokha pafupi pafupi? Ndi mfundo yodziwika bwino. Izo zikhoza kuchitika kenanso pompano pafupi ndi ife. "Oh," inu mukuti, "Ngati ndikadakhala moyo nthawi imeneyo, . . ." Chabwino, tsopano, ngati inu mukufuna kuti mudziwe chimene mukanachita nthawi imeneyo, muyang'ane chikhalidwe chanu cha panopa; ndipo inu mukhoza kuwona chimene mukanachita panthawi imeneyo, chifukwa izo ndithudi zikuulula.

34 Ophunzitsidwa kuti akhulupirire Mawu Ake, ndipo kenako pamene Mawu Ake anatsimikiziridwa pamaso pawo pomwe, iwo anawakana Mawu amene anatsimikiziridwawo. Pamene Mulungu anatsimikizira chimene Iye akanati adzachite, ndi kunena chimene Iye akanati adzachite, ndipo natsimikizira chimene Iye akanati adzachite, atatero iwo anatembenuka ndipo anamutcha munthu uyu "mzimu woyipa" (umene unawatemberera iwo onse). Taganizani za chimene chinachitika! Taganizani za chimene chinawapangitsa iwo; kuphunzira kwawo kunawapangitsa iwo kuti asawazindikire Mawu omwewo atasandulika thupi kwa tsiku lawo; maphunziro amene iwo anali nawo mmasukulu mwawo, ndi aphunzitsi abwino kwambiri.

35 Ndipo inu mukuti, "Chabwino, ife sitingachite zimenezo lero." Aphunzitsi awo anali opambana kwambiri kuposa athu lero (apamwamba, kani, kwa aphunzitsi athu), ndipo iwo analephera. Iwo analibe mabungwe naini handirede ndi nainte sikisi osiyanasiyana monga ife tiri nawo lero. Iwo anali nawo pafupifupi atatu. Ndipo mwa atatuwo, mutsike nawo atatuwo, ndipo palibe mwa atatuwo amene anawazindikira Iwo! Zikungosonyeza kuti zimene munthu amachita ndi zopusa kwa Mulungu. Mukuona?

36 Tsopano, iwo analephera kuti azizindikire Izo. Tsopano . . . Ndipo iwo achita chinthu chomwecho kachiwiri.

37 Munthu . . . Cholingacho ndi chabwino, nthawizonse chimakhala chabwino. Ndipo munthu samasintha kakhalidwe kake, samasintha njira zake mochuluka; ndikukamba za munthu wa padziko lapansi. Munthu nthawizonse amamutamanda Mulungu, munthu wachipembedzo, pa zimene Iye anachita, ndipo nthawizonse amawalozera anthu ku zimene Iye ati adzachite, ndipo kenako nkusalabadira zimene Iye akuchita! Mukuona? Ameneyo ndiye munthu basi, iye anapangidwa mwanjira imeneyo, wakhala ali chomwecho nthawizonse. Ndipo inu owerenga Baibulo usikuuno mukudziwa kuti izo ndi mogwirizana ndi Mawu, "kulondola." Iwo nthawizonse amamutamanda Mulungu pa zimene Iye wachita, nkumanena zimene Iye adzachite, ndipo nkusalabadira zimene Iye akuchita. Icho ndi chizolowezi basi cha munthu.

38 Chifukwa chimene iwo anachitira izi, aphunzitsiwo, mwa kuganiza kwanga tsopano: iwo anali atawatanthauzira Mawu, chifukwa iwo onse ankakhulupirira mwa Mesiya wakudza. Israeli yense ankakhulupirira izi, iwo amatero mpaka lero. Koma chifukwa chimene iwo sanamuzindikirire *Iye*, Uthenga Wake sunali wogwirizana ndi chovala chawo cha chipembedzo. Iwo . . . kutanthauzira kwawo kumene iwo anali nako kwa Mawu, Mesiya sanadziwonetsere Yekha mwa njira imene iwo ankatanthauzira kuti Iye akanadzachita izo. Chotero, ndipo chomwecho, iwo sanamuzindikire Iye chifukwa Izo sizinagwirizane ndi kutanthauzira kwawo. Monga ndinanenera kale, ndipo ndikunenanso, "Mulungu samasowa aliyense kuti atanthauzire Mawu Ake. Iye ndi wodzitanthauzira Yekha."

39 Tsopano, Baibulo limati . . . Ndiloleni nditsimikizire kwa inu tsopano kuti icho ndi Choonadi. Yesaya mneneri, zaka seveni handirede ndi fifitini izi zisanachitike, Yesaya mneneri anati, "Namwali adzayima, ndipo adzabala mwana." Sindikukaika kuti aliyense mu m'badwo umenewo ankaganiza kuti mwana wawo wamkazi adzakhala mkazi ameneyo, chifukwa Yesaya ananena zimenezo. Koma, inu mukuona, izo zinadzachitika zaka seveni handirede mtsogolo. Koma pamene . . . Mulungu sankasowa wina aliyense kuti awatanthauzire Mawu Ake, pamene Iye ati adzachite izo, kapena momwe Iye akanadzachitira izo. Iye anati Iye akanadzachita izo, ndipo Iye anazichita izo!

40 Mulungu analonjeza kuti Iye . . . uko mu Yesaya, aponso, ine ndikukhulupirira mutu wa 28, pafupifupi ndime ya 18. Ndiponso mu Yoweri 2:28, kuti m'masiku otsiriza, zaka thuu sauzande zotsiriza, Iye akanadzatsanulira Mzimu Wake pa thupi lirilonse. Iye anati, "Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera. Anyamata anu adzawona masomphenya. Okalamba anu adzalota maloto." Ndi zinthu zimene Iye akanati adzachite, Yesaya anati, "Ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena ndidzayankhula kwa anthu awa, ndipo uwu ndiwo Mpumulo." Koma iwo sanamvere

Izo. Iwo anapukusa mitu yawo ndipo anayenda mozipatukira Izo. Iye anati, “Magome onse a Mulungu adzakhala odzaza ndi masanzi, ndipo sipadzakhala kanthu koyera.” Ndipo ngati icho si chithunzi cha Yerusalemu, ndi mpingo wa tsiku limenelo pa Mesiya wakudzayo, ndi chithunzicho lero chimodzimodzi. Zikungodzibwereza zokha.

41 Tsopano, Mulungu akanena kuti achita chinthu, Iye anachichita icho. Mosalabadira chimene wina aliyense akuganiza za icho, chimene aliyense akunena, Mulungu akayankhula za chinachake, Iye amakhala wokakamizidwa kuti atanthauzire Mawu amenewo Iyemwini. Ndipo kutsimikizira Kwake kwa Mawu ndi kutanthauzira kwa Iye Mwini. Zindikirani, kutsimikizira Uthenga wa Mesiya Wake. Iye analonjeza chimene Mesiya akanadzachita akadzabwera. Ndipo pamene Iye anabwera . . .

42 Ngakhale pamene anzeru akummawa anayang’ana kumwera chakumadzulo, kuchokera kumene iwo anali ku Babulo, ndipo iwo anawona nyenyezi yachifumu. Kodi mumadziwa kuti palibe chidutswa cha mbiriyakale, paliponse, chimene wofufuza aliyense (kumene iwo ankasunga ngakhale—a—nthawi pogwiritsa ntchito nyenyezi, munthu wamkulu amene ankaphunzira nyenyezi izi) . . . Palibepo mbiriyakale imene imanena kuti aliyense wa iwo anaiwona nyenyezi imeneyo nkomwe. Chifukwa chiyani? Iyo siyinaperekedwe kwa iwo, iwo sankayembekezera zoterozo. Koma amuna anzeru awa ankadziwa kuti padzakhala Nyenyezi ya Yakobo idzawuke, ndipo iwo ankaiyembekezera Iyo, ndipo Iyo inadutsa kuyambira nthawi imene Yesu anabadwira ku Betelehemu . . .

43 Tsopano, ine ndikudziwa miyambo yathu ya Chikhristu, basi ili ngati mipingo yathu, iyo yasemphanitsa zinthu. Inu mupite kunja kuno ndipo mukawawona anzeru akubwera kudzapembedza khanda; mulibemo chinthu choterocho mu Lemba. Zaka ziwiri mtsogolo iwo anafika kumeneko, akutsika kudutsa mu zigwa ndi kuwoloka Mtsinje wa Tigris. Iwo samabwera kuti adzapembedze khanda, koma mwana wamng’ono wa pafupifupi usinkhu wa zaka ziwiri. Chifukwa chiyani zinali choncho, nthawi yomweyo, Herodi anapha ana onse kuyambira zaka ziwiri kumatsika mmusi? Kuti amupeze Mesiya. Inu mwaona, iwo . . . Mulungu anali atatsimikizira mwa Mawu Ake.

44 Ndipo pamene amuna a nzeru awa anafika ku Yerusalemu . . . Nyenyeziyo inawatsogolera iwo kupita ku likulu la chipembedzo padziko lapansi, Yerusalemu. Ndipo atangolowa pa zipata zija, nyenyezi ija (yauzimu imene inkawatsogolera iwo) inakana kuwawonetsa iwo kenanso. Chokwera ndi chotsika mmisewu amuna abwino awa, munthu wachuma wokhala ndi ngamila zokutiridwa bwino, ndi zina zotero . . . chokwera ndi chotsika mmisewu akuti, “Ali kuti Iye amene wabadwa ali

Mfumu ya Ayuda. Ife tinaiwona nyenyezi Yake kummawa." Ndipo likulu lalikulu la chipembedzo limenelo, zitatha zaka ziwiri za Uthenga wa abusa, linali likanalibe yankho kapena silimadziwa kalikonse za Iwo. Mkulu wa zipembedzo zonse analibe yankho.

45 Chotero izo zinasokoneza Sanhedrin, ndipo anayitanitsa Alembi kuti abwere adzawerenge. Ndipo iwo anawerenga nkhani ya Mika, mneneri amene anati, "Iwe Betelehemu, kodi iwe si wamng'ono mwa akalonga onse a Yuda (wochepetsetsa), koma kuchokera mwa iwe mudzabwera kazembe amene adzalamulire anthu Anga, Israeli." Ndipo atatha kuwerenga Malemba (ndipo akutsimikiziridwabe pamaso pawo), iwo sanavomerezebe Iwo, ngakhale Lemba linanena chomwecho. Ine ndikukayikira kwambiri kuti iwo angatero lero, ngati Malemba amene analonjezedwera tsikuli atati awonetseredwa. Ine mwina sindidzalalikiranso kwa inu kenanso, koma ine ndikufuna kuti inu mumvetse izi. Komabe iwo sangazikhulupirire!

46 Nzeru yaikulu ya Atate imapangitsa nzeru za munthu kukhala zopusa kwambiri mpaka Iye amamuchepsya munthuyo. Iye kwenikweni amafika pamalo pomwe zimamupangitsa munthu kudzichitira manyazi yekha, ndipo iye samakhala wamkulu mokwanira kuti avomereze kuti iye ndi "wolakwa." Iye amakhalabe ndi nkhani yakeyo, ziribe kanthu momwe Atate angatsimikizire kuti Mawu Ake ndi owona ndipo Iye akungochita zimene Iye analonjeza kuti adzachita. Munthu amaganiza kuti nzeru zake ndi zapamwamba kwambiri kuposa za Mulungu, ngati izo sizikubwera molingana ndi nzeru zake, "Chifukwa chiyani, Iwo si choncho." Zimenezo ndi zoona mu m'badwo uliwonse, zimachitabe zimenezo. Mukuona momwe nkhani yonseyo inkalumikizirana, tsopano?

47 Ndi kudzoza kotani kwa olishya amenewo! Angelo akubwera kumeneko kudzayankhula kwa olishya, Angelo a Mulungu akubwera kudzayankhula kwa gulu la abusa.

48 Ine ndikudabwa ngati inu munayamba mwakhalapo ndi mwayi wo—woyankhula ndi m'busa kapena kukhalapo naye mmodzi, kwa kanthawi? Ngati mungatero, ine—ine sindikufuna kunena izo chifukwa cha ndemanga yanga imene ndikufuna kuti ndinene pakapita kanthawi, koma m'busayo amakhala ndi nkhosa kwambiri mpaka amasekerera monga nkhosa (ikamalira), iye amayankhula monga nkhosa, ndipo amanunkha monga nkhosa. Uko nkulondola, chifukwa iye amakhala ndi nkhosazo. Ndizo zonse zimene iye amadziwa, ndi nkhosa zakezo.

49 Tsopano, Mawu otsimikiziridwa a Choonadi. Pamene abusa awa, odzichepetsa, amuna osaphunzira. . .Ndi ulemu bwanji, ndi zoyenera bwanji kwa m'busa kulandira uthenga wa nkhosa yobadwa kumene. Iwo sukanafikira kwina koma kwa abusa. Ndi chifukwa chimene Iye anabadwira mu khola, osati

mnyumba. Nkhosa sizimabadwira mnyumba, kapena mchipinda cha mchipatala chokongoletsedwa ndi pinki. Mukuona? Izo zimabadwira mkhola, ndi mminda.

50 Ndi chifukwa chake Iye *anatsogoleredwa* ku Kalvare. Simungaipangitse nkhosa kuyenda panjira yopita kokaphedwa. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Ku malo ophera nyama, iwo amakhala ndi mbuzi imene imatsogolera nkhosa. Ndipo iyo ikafika pamene malo ophera ali, imadumpha ndi kuilola nkhosayo kuti izipitirira. Nkhosa imayenera kutsogozedwa, iyo siingadzitsogolere yokha. Chotero, chomwecho, ankayenera kukhala m'busa akubwerera a. . .nkhosa yake. Pamene iwo anamupeza Mulungu-khanda ndendende kumene wa mthenga ananena kuti Iye akanadzakhala, ndipo pamene iwo anapeza Uthenga uwu wa mthenga modyeramo ziweto, ndendende pamene Mngelo anati Izo zikanadzakhala.

51 Tsopano, ndamvapo anthu akuti, "Mngelo anayankhula ndi ine, Iye anati, '*zakuti* ndi *zakuti*.'" Zimakhala zopusa bwanji nthawiyina; ndipo ndamvapo anthu akunena kuti Mngelo anayankhulana ndi iwo, ndipo anawauza iwo "*zakuti* ndi *zakuti*" zimene zinali mwamtheradi zotsutsana ndi Mawu. Tsopano, Mngelo angachite bwanji zimenezo? Izo sizingatheke basi. Ndipo ngati Mulungu anakuuzani inu kuti chinthu *chakuti-chakuti* chidzachitika (inu *mukuti* Iye anakuuzani inu), ndipo izo nkusachitika, ndiye sanali Mulungu anayankhula nanu. Ingokumbukirani, uko nkulondola. Mulungu samanama. Iye samapezeka mu bodza.

52 Pamene iwo anakamupeza Mwanayo, chiyenera kuti chinali chisangalalo chotani kwa iwo. Chifukwa Mngelo amene anawapatsa iwo uthengawo, iwo anazipeza izo ndendende momwe Mngelo ananenera momwe izo zidzakhalire, ndipo basi pamalo amene Mngelo anati izo zikanadzakhala. Icho chiyenera kuti chinali chinthu bwanji kwa iwo!

53 Modyera, bwanji? Mukuona momwe olishya awa anadekhera mu kholalo? Kodi inu mukuganiza kuti wa fioloje akanakhala chotani mmenemo? Iye akanayika chotchinga pamphuno pake, ndikuti, "Ndichotseni ine pamalo pano." Mukuona? Iye akanakhala kuti ali pamalo olakwika kwambiri, iye akanakhala momvetsa chisoni.

54 Koma, inu mwaona, izo zinali "kwawo basi" kwa m'busa. Mulungu amadziwa kumene angatumize Uthenga Wake. Mukuona? Kulondola ndendende basi. Mu chikhalidwe ichi chimene abusa analimo ndiye, mu khola lawo ndi Mwanawankhosa wawo, Uthenga wotsimikiziridwa umene iwo anaumva. Ndi zokongola bwanji! Mu kukhalapo kwa Mesiya, Mawu otsimikiziridwa a Uthenga wawo. Pamene abusa anamva kuti Mesiya ali padziko lapansi, ndipo anabwera mu kukhalapo Kwake, anabwera mu chikhalidwe chawo chomwe,

(ndipo anapeza kuti Uthengawo unali woona, unatsimikiziridwa pamenepo) zimenezo ziyenera kuti zinawapangitsa anthu amenewo kumverera motani, kukapeza kuti Mulungu anawachitira chinthu chachikulu ichi.

55 Bwanji, ophunzira akanakhala kuti ali pamalo olakwika kwambiri pamenepo, mu zochitika zoterozo, iwo akanachokapo mofulumira. Chifukwa chiyani? Wa Mthenga akubwera kwa olishya awamba. Mwinamwake sakanakhala nkomwe. . . awa . . . Ena mwa olishya awa mwina samatha nkomwe kulemba mayina awo omwe, zokayikitsa kwambiri. Inu mukudziwa olishya amene Yesu anawasankha pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, kuti azisamalira nkhosa Zake, "Kodi umandikonda Ine, Petro, kuposa awa?"

56 "Eya, Ambuye, Inu mukudziwa kuti ndimakukondani Inu."

57 "Dyetsa nkhosa Zanga." Ndipo Baibulo limanena kuti Petro anali mbuli ndi munthu wosaphunzira. Akusankhabe azibusa.

58 Mamembala a mpingo a masiku apitawo, ndi ansembe, ndipo gulu lophunzitsidwa bwino mu tsiku limenelo likanakhala pa malo olakwika kwambiri mu khola. Tsopano, ine sindiri wotsimikiza kwenikweni kuti ambiri a inu mungathe kumvetsa (mwinamwake, inu anthu a mumzinda) momwe khola la Chiyuda linkanunkhira, momwe ilo linkawonekera, monga nyama za khola limenero, ndi momwe ilo likanakhalira. Bwanji, ena mwa apamwamba amasiku anowa akanakhala kuti ali pa malo olakwika pamenepo, iwo—iwo sakanalowa ngakhale pakhomo. Koma izo zinamukondweretsa Mulungu, mwa nzeru Zake zopanda malire, kuti aziwulule Izo kwa iwo amene akanati adzazilandire Izo. Ophunzira, ndi amuna anzeru a tsiku limenelo sakanalandira Iwo. Iwo akanachititsidwa manyazi kwambiri kuti apezeke pa malo oterowo.

59 Bwanji, malo oyambirira, ngati iwo akanati abwerere ku mpingo wawo, ndipo akanachitira umboni kuti iwo anapezeka pa msonkhano woterowo, ndipo anakhulupirira gulu la azibusa osaphunzira amene amabweretsa chochitika chotero, iwo akanachotsedwa mu mpingo wawo. Iwo akanaponyedwa kunja kwa gulu la ku Betelehemu, ngati iwo akanagwidwa akumvetsera gulu la anthu osaphunzira monga momwe azibusa awa ankachitira. Kuchititsidwa manyazi, iwo ndithudi akanatero. Ngati iwo akanakhala kuti akuyanjana ndi anthu wamba amenewo, ndi kukhala. . . kuvomereza mipatuko yoteroyo ndi kukhulupirira kuti Mulungu angabweretse Uthenga Wake kwa gulu la azibusa osaphunzira, pamene iwo anali ndi chirichonse chokonzekera icho. Iwo akadataya mgwirizano wawo, iwo akanayenera kupereka mapepala awo, ndipo sakanakhoza kuzindikiridwa pakati pa dera la magulu awo a tsiku limenelo; chifukwa iwo analumikizana ndi chinthu choterocho, ndipo osati ndi malingaliro abwinoko.

60 "Ungayerekeze bwanji iwe!" wansembeyo akananena. "Iwe ukubwera mu malo anga opatulika awa ndi zampatuko zoterozo, ndi kupusa koteroko, kuti munthu wina wosaphunzira wakuthengo kunja uko amene sama. . .sanapite ku. . .kudutsa mu zophunzira zoyambirira. Ndipo nkukhulupirira uthenga woterowo, kuti, 'Mngelo anatsika ndipo anayankhula nawo'?"

61 Koma bwanji ngati munthuyo akanati, "Ine ndinawona Uthenga wake ukutsimikiziridwa"?

62 Iye akanati, "Dikira ndikupatse mwachangu mapepala ako. Ndipo tuluka mu gulu ili!" Nthawi zimasintha, koma anthu samasintha. Izo mwinamwake zikhoza kuchitikanso lero, iwo akanaponyedwera kunja kwa matchalitchi awo.

63 Koma azibusa anamverera kumasuka kwathunthu pa malo amenewo ndi Mwanawankhosa wa Mulungu. Ndipo m'busa wabwino aliyense amachita chinthu chomwecho. Pamene m'busa wabwino pa nkhosa akhoza kuwawona Mawu a Mulungu akumveka bwino ndipo akutsimikiziridwa, za chimene Iye analonjeza kuti adzachita, m'busa ameneyo wafika kwawo. Ine sindikusamala chimene wina aliyense akunena, pali "Mulungu analonjeza Izo, ndipo Mulungu anachita Izo."

64 Iwo amati, "Masiku a zozizwitsa anapita. Palibe chinthu chotero ngati Ubatizo wa Mzimu. Palibe chinthu chotero ngati Ubatizo wa Mzimu Woyera, izo zinali za atumwi."

65 Koma mulole m'busa woona wa Mawu alalikire Izo, mu mphamvu ya chiwukitsiro, kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Petro ananena pa tsiku la Pentekoste, "Lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale ambiri amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana." Kulikonse kumene Iye ayitane, lonjezo ndi dalitso lomwelo ndi lowona. Ndipo mulole m'busa weniweni wodyetsa Mawu awone zimenezo zikutsimikiziridwa, a fioloje onse pa dziko lapansi sangathe kuwachotsa Iwo kwa iye; chifukwa iye amadziwa kuti Mulungu ananena chomwecho, ndipo zichitika. Ndizo zonse. Iwo ndi Mawu a Mulungu nthawizonse. Mawu Ake anasandulika thupi ndipo anali akukhala pakati pawo, ndipo iwo samawadziwa Iwo.

66 Iye analonjeza chinthu chomwecho mu tsiku ili. Ine ndikudabwa ngati ife tingawazindikire Iwo? Onyada ndi anzeru anali asanalandirepo chinthu ngati chimenecho. Ndipo iwo ankakhulupirira kuti ngati pakanakhala chinthu chotero chonga Mesiya pa dziko lapansi, Icho ndithudi chimayenera kubwera ku chipembedzo chawo. Ilo likanakhala gulu lawo lomwe likanalandira Icho, kapena "Sizinali zolondola." Tsopano, tangoganizani molimba. Ngati izo siziri mu gulu lawo, ndiye. . .Kodi inu munazindikira, ndiye? Mulungu sanasankhe aliyense kuchokera mu gulu lawo, koma Iye anasankha amene sanalumikizidwe ndi chirichonse cha izo. Chifukwa gulu

limodzi likanati, "Mukuona chimene ife tachita?" Ndipo iwo akanachitanso chimodzimodzi lero. Koma Mulungu amasankha anthu wamba, ndi chifukwa chimene Iye anasankha m'busa. Azibusawo anali kwathunthu kwawo ndi Mulungu-mwanawankhosa ali pakati pawo, Mawu Ake akusandulika thupi pakati pawo. Onyada ndi anzeru sanalandire konse Iwo, anawalambalala iwo.

67 Ndipo ife tikhoza kunena zochuluka chomwecho za lero, kapena mu m'badwo uliwonse. Izi zinali zinthu zomwezo mmasiku a Martin Luther. Chinthu chomwecho mmasiku a John Wesley. Zinali zinthu zomwezo mmasiku a Achipentekoste. Koma Mulungu sayimira bungwe lamunthu! Iye amawusunthirabe Mzimu Wake patsogolo kuti akatsimikizire Mawu Ake! Icho chimayenera kukhala ndi kubwera mu gulu la bungwe lawo lomwe apo ayi iwo sakanawalandira Iwo. Pamene iwo ali aliwuma lero, mipingo yonse, kuti iwo "akachita *chakuti-ndi-chakuti,* ndi kulumikiza mipingo yonse pamodzi." Ngati iwo akufuna wa mthenga tsopano, yemwe angawalumikize Achiprotestanti onse, Akatolika ndi Orthodox, chirichonse pamodzi, kupanga mpingo umodzi waukulu.

68 Tsopano, abale, ndakhalapo nawo mwayi wolalikira kwa ma handirede a zipembedzo zosiyanasiyana, ndipo muli anthu abwino mu zonsezo. Koma tsopano, inu kumbukirani, ine ndikulosera, "Bungwe lirilonse lidzayenera kuvomereza izi, apo ayi silidzakhala bungwe. Ndiko kukukakamiza iwe." Kodi inu munawerenga pepala la Tucson lero kumene ansembe Akatolika amathandizira kudzoza, mu pepala. . . kuthandizira kudzoza, ku Missouri, m'busa wa Chiprotestanti? Ndipo ndi ndani amazizindikira izo? Apresbateria, Abaptisti, Alutheran, ndi Assemblies of God. Izo ziri mu pepala la Tucson lero.

69 Oh, ndi zodzidzimutsa! Izo si munthuyo mmenemo, ndi atsogoleri achipembedzo, atsogoleri aboma amene akupotoza chinthucho mmenemo, kachitidwe kamene kamakuponyerani inu mu izo kaya mukufuna kapena ayi. Inu simungakhale konse bungwe nkudzathawa mkwiyo umene ukubwera pa dziko lapansi, ndipo mudzawona ngati izo sizoona. Ine ndikhoza kudzakhala nditapita pamene izo zizidzachitika, mudzayang'ane mmbuyo pa imodzi ya matepi awa. Ndiyeno ngati izo sizinali choncho, ndine mboni yonama. Ngati zinali choncho, ndanena Choonadi.

70 Iwo akanakhoza kuchitcha Icho "mtundu wina wa kugwira ntchito kwa mzimu woyipa" motsutsana ndi kuganiza kwawo kwabwino. Inu mumamva zochuluka kwambiri lero za kuganiza kwabwino: muzingoyika malingaliro anu pa chirichonse, ndi kumaganiza mwabwino za izo. Mdierekezi akhoza kuchita zimenezo! Pali chinthu chimodzi chokha chimene chimalamulira zonsezo, ndipo ndicho Mawu a Mulungu. Ngati

inu mukuganiza motsutsana ndi Mawu, muyiwale kuganiza kwanuko. Muziganiza pa Mawu.

71 "Mesiya," iwo ankaganiza, "sangapezeke mmalo oterowo, anyansi ngati amenewo."

72 Kodi inu mungaganize wabwino, wansembe wopambana wamkulu, kapena mkulu wa mpingo, wopukutidwa mu fioloje, angabwere kumusi ku khola lodzadza ndi ndowe? Ndi kudzalandira Uthenga wa m'busa wosauka, wodzichepetsa amene analibe maphunziro, ndipo angabwere ndikudzati "Mwaona, ine ndikhoza kutsimikizira Iwo kwa inu, uyu ndi Mwana, uyu ndi wa Mthenga"?

73 Ndipo inu mukudziwa chimene anthu amenewo akananena? "Mwamunayo ndi woona, iye ndi woonamtima pa chimene Iye akunena, koma iye akulakwitsa mwamtheradi!"

74 Ine ndawawonapo anthu akukhala miyoyo yabwino mpaka anthu osakhulupirira, osatha kunena chirichonse chokhudza iwo, koma iwo amati "Iye akulakwitsa moonamtima. Iye sakudziwa basi chimene akunena. Mulungu, Iye sangachite chinthu ngati choterocho."

75 Koma apa iwo anali ndi umboni! Ndipo utatha umboni, "Pitani uko ku khola ndipo mukaone ngati Mwana ameneyo sakugona kumeneko."

76 Iwo akanati, "Iwe walodzedwa ndi mzimu wina woyipa, umene wakupangitsa iwe kunena ichi." Komabe izo zinali molingana ndi Mawu a Mulungu! Ndipo iwo anali akhungu kwambiri kuti awone Iwo, chifukwa fioloje yawo inali itawachititsa khungu iwo. Ndi zangozi bwanji!

77 "Anapezeka mmalo oterowo? Mu nyansi zonga zomwe izi zinali? Mu khola?" Pamene iwo anali ndi malo okongola akuti Iye abweremo, iwo anali atakonza chirichonse kuti Iye adzabweremo, ndiyeno kuganiza kuti Iye akanadzatsika (ndi kupita) ndipo osawabweretsera aphunzitsi awo Uthenga. "Ndipo kodi angawupereke Iwo kwa gulu la abusa osaphunzira? Ndiyeno nkumubweretsa Mwana Wake yemwe, ndi kuti Iye abadwire mu—khola? Khola la akavalo la wamba? Chabwino, mu—modyera msipu? Bwanji, sizikanakhala chomwecho!" Iwo sakanakhulupirira Iwo, chifukwa Iwo anali odzichepetsa kwambiri.

78 Ndipo Iwo ndi ophweka kwambiri, ndi momwe anzeru nthawizonse amawalambalala Iwo. Iwo ndi ophweka kwambiri, Iwo amawadodometsa iwo. Iwo ankafunafuna njira ya Mulungu kunja uko, pamene Iye anali pomwepo. Mukuona? Iwo akufunafuna chinachake kutali, pamene icho chiri pomwepa ndi iwo tsopano: Khristu, anawuka kwa akufa, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

79 Zinthu zawo zonse zazikulu zinalambalalidwa. Koma izo ndithudi zinali Choonadi, kuti "pamenepo panali Mesiya." Ife tikudziwa zimenezo lero. Ife tikuzikhulupirira zimenezo lero. Ife tikuzivomereza zimenezo lero.

80 Komano ngati Mulungu analonjeza chinachake pa Khrisimasi iyi, analonjeza chinachake cha tsiku lino, ndipo akutsimikizira kuti Ndi choncho, ndipo ife tikuyendabe kuchoka kutali kwa Iwo, ife basi tiri mu gulu lomwelo limene iwo anali (kumbuyo uko pa tsiku limenelo) amene anawalambalala Iwo; chifukwa Iwo sa—samabwera mwa kukoma kwathu kwa chipembedzo. Ndi chifukwa chake tiri mu chisokonezo chachikulu pa Khrisimasi iyi.

81 Yesu Khristu si wakufa, Iye ali moyo. Iye ali pano lero! Baibulo linati, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Iye ananena, mu Yohane Woyera 14:12, "Iye amene akhulupirira pa Ine . . . " (osati iye amene amadzipangitsa kukhulupirira, iye amene *anena* kuti amakhulupirira) "Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iye adzazichitanso. Ndipo zochuluka zoposa izi adzazichita, chifukwa Ine ndikupita kwa Atate." Ndipo ine ndamuwona Iye, mmoyo wanga womwe, akuchita zochuluka za ntchito zomwezi (zimene Iye anachita nthawi imeneyo) kuposa zimene zalembedwa mu masamba a Baibulo ili. Ndipo izo zikuwadutsa pamwamba pa mutu ndi anzeru lero, ndipo zikuwululidwa kwa makanda amene angaphunzire; monga Yesu anapempherera. Izo ndi zoona, Iye anachita zochuluka kuposa Iye . . . Ine ndaziwona mu tsiku langa, za zaka sarte-firii za utumiki, ine ndamuwona Iye akuchita zochuluka kuposa zomwe ine ndawerenga za Iye akuchita mu Baibulo; zochuluka za chinthu chomwecho.

82 Koma ziribe kanthu chimene Iye anachita nthawi imeneyo, kodi mukuganiza kuti Sanhedrin inamukhulupirira Iye? "Chabwino," iwo anati, "iwe walodzedwa." Koma, fufuzani, pamene iwo analakwitsira panali kupeza . . . pofufuza, osati chimene kachikhulupiriro kawo kankanena, koma chimene Mawu anati Mesiya akanati adzachite mu tsiku lawo. Ndipo pamenepo ndi pamene ife timalakwitsira lero, posamafufuza Malemba. Yesu anawawuza iwo, "Fufuzani Malemba, mwa Iwo inu mukuganiza kuti muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Iwo ndi Amene akuchitira umboni za Ine. Iwo amakuwuzani inu Chimene Ine ndiri."

83 Zindikirani, Mulungu anadziwiratu kuti iwo akanadzachita izi, ndicho basi *chifukwa* Iye ankayenera kuwutengera Iwo kwa abusa. Iye ankadziwa kuti iwo sakanachita izo, iwo sakanaulandira Iwo. Tsopano kodi inu mukuona chifukwa chimene ankayenera kukhala azibusa? Chifukwa chiyani azibusa? Afioloje sakanaulandira Iwo. Chifukwa chiyani azibusa kenanso? Kodi Izo zingabwere motsutsana ndi Mawu Ake? Ayi! Iwo anali azibusa, iwo ankadziwa nkhosa; ndipo ndi

chimene Iye anabadwa, nkhosa, mwanawankhosa. Zindikirani, Iye anali Mwanawankhosa. Iwo anali—iwo anali mtundu wokhawo umene ukanamulandira Iye. M'busa anali chinthu chokhacho chimene chikanalandira Mwanawankhosa. Iwo ankadziwa momwe angasamalire Iwo, ndipo chomwechonso izo ziri lero pamene ife tikulandira Uthenga wa Mwanawankhosa.

84 Tsopano chokhudza! Munthu wodzichepetsa kwambiri, wosaphunzira kulambira Emanuele mu khola. Kwambiri... Ndipo uko kunali anthu kunja uko, mmasiku omwewo, akuphunzitsa fioloje yawo. Khamu lalikulu, likukoka ponseponse, kuchokera konsekonse mdzikolo, iwo amabwera kudzapereka nsembe zimene Yehova anati zinali "zonunkha m'mphuno Zake." Ndipo apa panali azibusa odzichepetsa, mu khola, akulambira Emanuele; Mulungu Mwiniwake atasandulika thupi, ndipo atagona mu khola. Mukuona, momwe ife ndi kuphunzira kwathu kwakukulu, ndi mutu wathu titawudzutsa mmbuyo ngati kuti tikudziwa chinachake, ndipo Mulungu amachilambalala chinthu chonsecho. Mukuona? Iye amachita zimene Iye amalonjeza kuti adzachita, ndipo Iye nthawizonse amachita zimenezo. Koma taganizani za azibusa otsika awa kunja uko tsopano akupembedza Eman-... Emanuele mu khola. Ndi zokhudza kwambiri. Ndithudi ziri!

85 Ndiye kunja...Atatha kumupembedza Iye, ndipo atazindikira kuti Uthenga umene iwo ankalalikira unali utatsimikiziridwa, pamenepo iwo ali...anali uko akumutamanda Mulungu ndi Uthenga wodabwitsa kwambiri wa Mngelo. Tsopano mufanizitse zimenezo ndi lero. Mungoyima miniti ndipo muganize. Munthu uko akumutamanda Mulungu, ndi kumulemekeza Iye chifukwa cha zimene iwo anawona, zimene iwo anamva, zimene iwo amadziwa kuti ndi Choonadi, ndi Uthenga umene unali wodabwitsa kwa malingaliro aluntha. Iwo unali wotsutsana ndi malingaliro onse achipembedzo, ndipo komabe icho chinali Choonadi! Ndi Choonadi! Iwo anawukhulupirira Iwo. Ndipo tsopano, nzeru za munthu zingakhale zopusa bwanji! Kenako nkumanena kuti kwayara ya Angelo inawaimbira iwo nowelo yoyamba. Kodi inu mungaganizire zimenezo? M'busa uja amene samatha kulemba dzina lake, akununkha ngati khola la nkhosa, akuyenda mu msewu, akufuula, "Ulemelero kwa Mulungu wa Mmwambamwamba! Tikudziwa kuti Iye ali padziko lapansi!"

86 Wansembeyo anati, "Mwamuna ameneyo ndi wamisala. Tayang'anani pa mabukhu ndipo muwone ngati iye ali membala wa mpingo wathu. Iye ndithudi akutichititsa ife manyazi ndi zophunzitsa zake zosayenera. Mchotseni iye kwa ife. Ife sitichititsidwa manyazi pakati pa anthu."

87 Chabwino, mukhoza kuchititsidwa manyazi pakati pa anthu ndi kulemekezedwa pamaso pa Mulungu; kapena kutenga chisankho chanu, chifukwa, kumbukirani, zokonda

za matchalitchi a tsikuli sizigwirizana ndi Mawu a Mulungu. Palibe kukoma kosiyanasiyana naini handirede ndi sikisite naini kwa Iwo. Kulipo kukoma kumodzi, Mawu amodzi, Mulungu mmodzi. Ndizo zonse.

88 Akunena kuti Angelo anawaimbira nowelo yoyamba, komanso akumanena kuti "tinalandira Uthenga kuchokera kwa Mngelo." Mngelo anawonekera kwa iwo, anawapatsa iwo Uthenga, ndipo anapita ndipo anakapeza kuti Uthenga umenewo unali Choonadi. Ndipo akuti, "Pambali pa zimenezo, Mngelo anayimba nowelo yoyamba kwa ife."

89 "Kodi inu mungalingalire?" Iwo anati, "Munthu wosauka ameneyo." Iwo sakanafuna kukhala ndi chirichonse chonga icho kuti chichitike pakati pawo, inu mukudziwa, chotero icho chinali ngati chiphunzitso chachilendo kwa iwo. Ndipo ndi chifukwa chake iwo samawapeza Iwo m'Malemba, sizinali za iwo kuti awapeze Iwo. Zodabwitsa kwa anzeru, kunalibe chowachitikira chotere chimene chinachitika kwa iwo. Zosakhulupirika, komabe Icho chinali Choonadi. Icho ndi Choonadi, ife tikudziwa Icho ndi Choonadi. Taganizani! Otembenuka mtima oyamba ndipo mpingo woyamba unali oweta nkhosa, osati atsogoleri achipembedzo; oweta nkhosa, azibusa. Chifukwa chiyani azibusa?

90 Zindikirani! Kumeneko akumutamanda ndi kumulemekeza Mulungu chifukwa cha chimene iwo anali atawona ndi kumva, anawamva Angelo akuyimba kwa nthawi yawo yoyamba kwa munthu. Angelo anali asanamuimbirepo munthu nkale lonse. Ndipo kuyang'ana pa makwaya, momwe iwo anali atayimira ndi kuphunzitsidwa ndi kuphunzitsidwa mawu amenewo, "iwo akayimba pa kubadwa kwa Mesiya," ndipo iwo onse analumphidwa! Ndipo Angelo anatsika pansi ndipo anadzayimba kwa abusa wamba, osati atavala zovala za tchalitchi, koma atavala zovala za ubusa. Ndipo taonani amene analandira Uthenga woyamba, ndi zodabwitsa.

91 Ndipo kumene iwo unaperekedwa, osati mmatchalitchi, koma mchipululu, kunja mu chipululu kumene Mngelo wa Ambuye anabwera. Osati mu tchalitchi, mchipululu. Iye sanalandiridwe nkomwe mu tchalitchi. Iwo ankaganiza kuti Iye anali, ndipo iwo ankaganiza kuti iwo anali ndi Iwo, koma Mulungu anatsimikizira kuti izo zinali zolakwika. "Iye ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu." Uko nkulondola.

92 Nthawi yoyamba imene Angelo anaimba pa chikondwerero, kunali Kumwamba. Ngati inu mungayang'ane pa Yobu 38:7, (monga ndikuwona ena a inu mukulemba zolemba), pamene Mulungu anakonza koyamba za kupanga chirengedwe Chake choyamba, dziko lapansi. Yobu anali munthu wopambana, wanzeru, ndipo anali ndi nzeru za mitundu yonse. Iye

anati, “Ndikapita ku misika, akalonga achichepere, iwo onse amadzagwada pamaso panga, ndipo amangofuna kamphindi ka nzeru zanga.” Ndipo iye samatha kudziwa chifukwa chimene ankachitiridwa momwe ankachitidwira.

93 Ndipo chotero Mulungu anamufunsa iye, anati, “Dzimange mchiuno ngati mwamuna, chifukwa Ine ndikubwera kudzayankhulana nawe.” Ndipo pamene Mulungu anadzatsika mu kamvuluvulu, Iye anati, “Yobu, iwe unali kuti ine ndisanakhazikitse maziko a dziko lapansi? Pamene nyenyezi zammawa zinkayimba limodzi, ndipo ana aamuna a Mulungu nkumafuula ndi chisangalalo, iwe unali kuti ndiye, Yobu?” Ndipo iye anaphwetsedwa pa nthawi imeneyo. “Iwe unali kuti?”

94 Mwaona, nthawi yoyamba imene Angelo anayimbako pa chikondwerero, kunali Kumwamba. Koma nthawi yoyamba imene iwo anadzayimba pa dziko lapansi, inali kwa azibusa pa kubadwa kwa Mulungu, Emanuele pa dziko lapansi; anthu oyambirira amene anamvapo konse Mngelo akuyimba, anali azibusa odzichepetsa.

95 Pamene ife tiwatenga akazi athu openta nkhopewa, odula tsitsi, ovala akabudula, ndi kugwedeza mtundu wina wa mwinjiro wa tchalitchi pa iwo, ndi kuwaimitsa iwo ndi kumayimba ngati chinachake, ndipo zikatero ife timaganiza kuti Mulungu akuyenera kumvetsera zimenezo? Iye ali nawo Angelo kumbuyo uko amene angamusangalatse Iye kuyambira... Iye asanamupange konse munthu. Uh-huh. Kumapita uko ndi kumakakhala moyo...ndi kumakavala zovala zimene ziri zonyansa kwa Mulungu, ndipo inu mungayembekezere bwanji kuti zimenezo zingakhale za Mulungu? Inu mumati, “Chabwino, ine ndi wa...”

96 “Iwe unali kuti pamene ndinkaika maziko a dziko lapansi? Ndiuze Ine kumene ndinamangirirako ilo. Chiri kuti chitsulo chimene iwo amayatsa? Iwe unali kuti nthawi imeneyo?” Inu mumaganiza kuti Mulungu angatifunse ife nzeru zathu. Nzeru zathu ndi zopusa kwa Iye. Iye amachita chimene Iye wanena kuti Iye adzachita.

97 Tsopano zindikirani, Mulungu akukonzekera kuti apange chirengedwe china. Iye kulenga dziko lachivundi, moyo wachivundi. Angelo amayimba Kumwamba. Koma apa Iye akulenga Moyo watsopano, Moyo Wamuyaya wa munthu, ndipo Iye akuyimba kwa anthu Ake kudzera mwa Angelo; padziko lapansi, osati Kumwamba. Kumwamba kunali ndi Moyo Wamuyaya. Mukuona? Ndipo Iye anayimba...iwo anayimbira Miyamba, pamene chirengedwe chachivundi chinkabweramo; ndipo apa chirengedwe cha chisavundi chikubwera, ndipo tsopano iwo akuyimbira anthu a padziko lapansi. Nthawi yoyamba, kwa azibusa. Chodabwitsa, sichoncho izo?

98 Iye anali atayamba chirengedwe chatsopano. Icho chinali chiyani? Chirengedwe cha Iyemwini. Mulungu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu. Ndizo. . .Baibulo linati, "Pachiyambi cha chirengedwe cha Mulungu." Mulungu analengedwa mu mawonekedwe a munthu; mwa Yesu Khristu, Mwana Wake, Mulungu ankakhalamo. Iye anadzimangira hema Wake wa mnofu ndi mafupa, ndipo ankakhala mu kachisi ameneyo; Mulungu, *Emanuele*, "Mulungu nafe." Iye anadzimangira Yekha nyumba, kuti azikhalamo, kuti Iye adzakhoze kunyedzimiritsa Mawu Ake kwa omumvera Ake kudzera mu zimenezo. Inu mungadziwe chimene Mulungu ali, pamene inu mumuwona Khristu.

99 Kumbukirani, nthawizonse pamakhala kuyimba pa kubadwa kwa mfumu. Ndi angati amadziwa zimenezo? Ndithudi, inu mumatero. Chabwino, tsopano, kodi inu mukuganiza kuti ngati Mfumu iyi ikanabadwira kumusi uko, mzimayi akanabwera akuthamangira kudzalowa mu chitchalitchi penapake, ndikuti, "Konzani bedi msanga, ndipo tengani madokotala, chifukwa ine ndikudzabereka Emanuele kwa dziko lapansi"? Mkazi wosauka wochokera ku Nazareti, mzinda wotsikitsitsa, a. . .wankhanza kuposa Tucson kapena uliwonse wa iwo, ndipo komabe mkazi wamng'ono uyu akubwera akuthamangira kumeneko kwa wansembe wamkulu ndikuti, "Ine—ndikukonzekera kubereka Emanuele." Iwo akanamuponyera iye mu ndende. Iwo ndithudi akanatero. Iwo mwamtheradi akanatero. Za mpatuko ngati zimenezo kubweretsedwa pakati pa anthu ake, iye sakanaziyimira izo. Iye sangatero leronso. Koma chimodzimodzi zikuchitika, chimodzimodzi basi.

100 Zindikirani, pakuyenera kukhala kuyimba. Mafumu anali. . .Iye sibwenzi atayimbiridwa. Anthu sibwenzi atamuyimbira Iye, chifukwa iwo sankamukhulupirira Iye. Ndipo ndi chifukwa chake. . .Apa Iwo akubwera, inu mukhozanso kuwamvetsetsa Iwo. Ndi chifukwa chimene lero anthu amachita manyazi kutamanda Mulungu, amachita manyazi ndi Khristu! Matchalitchi akuluakulu sangalandire Ubatizo wa Mzimu Woyera, iwo ndi okhazikika kwambiri mu njira zawo za chitchalitchi mpaka kuti sangawulandire Iwo. Mulungu adzapeza winawake amene Iye angatamandidwe naye. "Iye ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu," momwe ndikubwereza za Yohane kachiwiri.

101 Zindikirani, omumvera Ake akuyenera kumuyimbira Iye. Ndipo omumvera Ake pamenepo anali Angelo Ake, ndipo iwo anayimba kwa azibusa Ake amene anali oti atenge Uthenga Wake.

102 Ndani akuyenera kuwumva Iwo poyamba? Ndithudi, omumvera Ake. Iwo ndi amene akanamva kuyimba kwa Mfumu koyamba, akanakhala omumvera Ake. Ndipo omumvera Ake

anali ndani? Zokhala ngati zokhudza, sichoncho izo, abale? Iwo sanali atsogoleri Ake achipembedzo. Sanali a fioloje. Uko nkulondola. Sanali anthu achipembedzo. Ayi, anali azibusa. Chifukwa chiyani? Panali nkhosa imabadwa, ndicho chifukwa chake. Mukuona? Omumvera Ake anawumva Iwo, amene Mulungu ankawadziwa kuti akhulupirira. Mulungu anatumiza Uthenga Wake kwa iwo amene akanati awukhulupirire Iwo. Iye ndi nzeru zonse; Iye amadziwa kumene angatumize Uthenga Wake, amene ati adzawukhulupirire Iwo. Wapamwamba kwambiri wa Kumwamba anatumizidwa kwa munthu wotsikitsitsa pa dziko lapansi.

103 Yesu anatero, mu Mateyu 5, "Odala ali osauka mu mzimu, chifukwa wawo ndi Ufumu wa Kumwamba." Maria, mu . . . Ngati mukulemba Malemba amenewo, ameneyo ndi Mateyu 5. Ndipo ngati mukulemba Malemba . . . Ndi zomwe ndalemba apa, ndi Malemba.

104 Maria anati, pa Luka 1:52, pamene iye anadzozedwa ndi Mzimu, Mzimu Woyera pa iye, iye anati, "Iye wawakweza iwo amene ali otsika." Maria ananena zimenezo, amake a Yesu, anati, "Iye wawakweza iwo otsika."

105 Luka ananenanso, "Anthu wamba anamumva Iye mokondwera." Osati—osankhika, a—a fioloje, madokotala a zamalamulo ndi umulungu; koma anthu wamba anamumva Iye mokondwera, anthu otsikitsitsa.

106 Kudutsa Mmalemba onse opatulika, Uthenga wa chiwombolo umaperekedwa ndi azibusa ndiponso kudzera mwa nkhosa.

107 Tsopano ine ndiyenera kufika potseka, chifukwa tikuyandikira nthawi yotsekera. Ine ndikulambalala Malemba ambiri kuti ndikufikitseni inu ku lingaliro ili.

108 Kudutsa mu Lemba lonse, chiwombolo chakhala chikuimiririridwa kudzera mwa azibusa ndi nkhosa. Uko nkulondola. Tonsefe tikuvomerezana nazo zimenezo. Bwanji? Iwo unali mu mthunzi ndi choimira. Ndipo chirichonse . . . Ngati sindinaliwonepo dzanja langa, ndipo nkuyang'ana pansi pa mthunzi wa dzanja langa, ndipo nkuwona kuti ndinali ndi zala zisanu, ine ndingadziwe kuti ilo likunyedzimiritsa; mthunzi umawonetsera chenicheni. Ndipo ndi chifukwa chake Uthenga nthawizonse umabwera kwa . . . chiwombolo kudzera mwa nkhosa, chifukwa kuyambira pachiyambi pomwe . . . Ndipo zinali kudzera mwa nkhosa, ndi azibusa, ndi momwe Iye ankadziululira Yekha. Zonse zinali mithunzi ndi zoyimira.

109 Tsopano tiyeni tiyang'ane pachiyambi. Adamu ndi Eva, atayima pamenepo pamaso pa Mulungu kuti amvetsere Uthenga Wake kwa iwo, iwo anali atadzikulunga mchiuno mwawo chikopa cha nkhosa. Uthenga woyamba umene unayamba wamvekapo, unaperekedwa pamwamba pa chikopa cha nkhosa

yakufa, imene Mulungu anapha ndi kumukulunga Adamu ndi Eva mmenemo. Atatha kuyesera kupanga chipembedzo chawo cha masamba a mkuyu, icho sichinagwire ntchito. Nsembe ya nkhosa inali itakhazikitsidwa ngati chitetezero kuyambira pachiyambi pomwe, nsembe ya nkhosa.

110 Tsopano, titsekera apa tsopano, ndi kukuwonetsani inu chifukwa chomwe iwo ankayenera kukhala azibusa; ndi chifukwa chimene izo zinkayenera kukhala, Iye ankayenera kukhala nkhosa.

111 Tsopano, aneneri a Chipangano Chakale ankadzikulunga okha mu zikopa za nkhosa (tikudziwa zimenezo, uh-huh), kuimira chikhulupiririro chawo mu Mawu Ake cha kudza kwa Mwanawankhosa wangwiro. Ndi chifukwa chake aneneri.

112 Tsopano, Mawu a Mulungu samabwera kwa wa fioloje, palibepo…iye—iye ndi amene amawasokoneza Iwo. Uko nkulondola. Palibe chinthu ngati chimenecho monga kunena… Inu mukuti, "Chabwino, munthu uyu ndi wa fioloje." Izo zimangomuika iye patali kwambiri ndi Mawu kuposa chirichonse chimene ine ndikuchidziwa. Mukuona? Mawu a Ambuye Mulungu, Mulungu wosasintha, samasintha konse. Paliponse mu Baibulo, Mawu a Mulungu nthawizonse ankabwera kwa aneneri. Osati kwa a fioloje kapena madokotala, kwa aneneri! Ndipo iwo nthawizonse, nthawi iliyonse, ankakanizidwa ndi kukanidwa.

113 Aneneri kawirikawiri amakhala abusa nawonso. Aneneri ankadzikulunga okha ndi zikopa za nkhosa, chifukwa ankavala chikopa cha nkhosa zomwe iwo ankaweta. Ndipo uthenga woyamba, kwa a—a—kam'badwo kotsutsidwa, unali pamwamba pa zikopa za nkhosa. Aneneri, ndikunena kenanso, ankavala zikopa za nkhosa atadzikulunga okha, chifukwa iwo ankachitira umboni ndi chimenecho, kuti iwo ankakhulupirira kuti kunali kukubwera Mwanawankhosa wangwiro wa nsembe imeneyo. Ndipo Mawu a Mulungu ankabwera kwa iwo pamwamba pa zikopa za nkhosa. Abusa awa…kapena aneneri amenewa kawirikawiri amakhala abusa. Abrahamu anali m'busa. Isaki anali m'busa. Yakobo anali m'busa. Mose anali m'busa. Davide anali m'busa. Oyimira onse a Mulungu kawirikawiri amakhala abusa.

114 Tsopano ife tifufuza chifukwa chimene iwo unabwera kwa abusa. Iwo ankadziwa kuti nkhosa zimakhala zopanda thandizo popanda m'busa kuzitsogolera. Iwo…nkhosa imakhala yopanda thandizo, iyo siingayende yokha. Ndi chifukwa chake Mulungu amawayerekezera ana Ake okhulupirira ndi nkhosa. Iwo amayenera kuti azitsogoleredwa. Koma onani chimene chikukutsogolerani inu! Musatenge mbuzi, idzakutengerani inu ku khola lokaphedwako. Mulungu sanatipatse ife mbuzi, Iye anatipatsa ife Mwana Wake (Mzimu Woyera) kuti azitilondolera

ife. Iye ndi Namulondola wathu, osati abusa ena opangidwa ndi munthu, koma m'busa-woperekedwa ndi Mulungu amene amazidyetsa nkhosa chakudya cha nkhosa.

115 Tsopano, inu muitenge nkhumba, ndipo nkunena kwa nkhumba imeneyi, "Ndikupanga iwe kukhala mwanawankhosa." Ndipo nkuyisambitsa iyo. Ndipo nkuyipenta zala zake zakumapazi, ndi—ndi zina zotero. Ndipo nkuyipatsa chakudya ngati nkhosa, kuyipatsa mtundu wina wa—chakudya. Ndipo nkuiyika iyo pansi kapena kunja mu. . .kumene a—gulu la nkhosa, mmunda wa msonthi kapena chinachake. Ndipo ngati pali dzenje lamatope paliponse, nkhumba imeneyo ingapite molunjika ku dzenje lamatope momwe ingathere. Mukuona? Bwanji? Ndi chifukwa chakuti chikhalidwe chake chikadali nkhumba.

116 Ndipo ndi chifukwa chake mamembala ampingo, lero, amachita zinthu za mdziko, mwaona, ndi chifukwa chakuti chikhalidwe chawo sichinasinthidwe. Iwo amadya mtundu uliwonse wa zatchalitchi, nyansi za fioloje, koma Mawu a Mulungu sangathe kupirira nawo Iwo. Iwo amakalowa ndi kukamvera Mawu. . .

117 Inu mukudziwa, wachinyengo wamkulu padziko lapansi, ndi khwangwala wokalamba. Mu Baibulo, panali ziwiri zimene zinatulutsidwa mu chombo. Khwangwala wokalambayo anatuluka ndipo sanabwererenso, chifukwa iye ndi khungubwe, khwangwala. Iye anakhazikika pa matupi a mitembo yokufa ndi kudzaza mimba yake ndi mitembo yakufayo. Koma pamene anadzaitulutsa nkhunda, nkhundayo sinathe kupirira kununkha kumeneko, chotero iyo inabwerera kunyumba ya Atate ndi Nowa, ndipo inkagogoda pakhomo mpaka Nowa anailowetsa iyo.

118 Tsopano, khwangwala akhoza kukhala kunja kuno ndi kudya pa kavalo wakufa, tsiku lonse, ndi kuwulukira kunja uko mmunda ndi kukadya tirigu ndi nkhunda. Koma nkhunda siingaulukire kumeneko ndi kukadya kavalo wakufa, ndipo kenako nkudya tirigu; izo zingayiphe iyo. Mwaona, nkhunda ilibe ndulu iliyonse, ndipo iyo siyingazigaye izo.

119 Ndipo pamene nkhunda iliyonse ya Mulungu, nkhunda iliyonse yakudya Mawu kapena nkhosa, nyama yoyera, mukapita kukawapatsa iwo zinthu za dziko lapansi, amadziwa kuti Mbuye wawo anati, "Iye amene akonda dziko lapansi kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa iye." Inu mukampatsa iye chinachake chosiyana ndi Mawu a Mulungu amenewo, iye sangapirire nacho. Koma mdierekezi akhoza kutenga Icho ndi dziko nalonso, ndi kudzitcha izo zonse za Mulungu. Inu simungasakanize mafuta ndi madzi, sizingasakanikane.

120 Iwo, azibusa onse awa, ankadziwa kuti nkhosa imakhala yopanda thandizo popanda m'busa. Ndipo iwo anali azibusa, ndipo ankadziwa kuti iyo imayenera kulondoleredwa.

121 Ndi zomvetsa chisoni bwanji kuziwona, lero, kuti iwo amayesetsa kumazidyetsa nkhosa, nyansi. Koma nkhosa sizingadye zimenezo. Ayi, bwana! Mwaona, iwo ankayesetsa kuzidyetsa nkhosa, kumbuyo uko, nyansi. Ndipo pamene Mawu amabwera, iwo anali atazolowera nyansizo, iwo sanawadziwe Mawu. Ndipo ndizo zimene ziripo lero, pamene chinthu chomwecho chotsimikizika ndi kuwonetseredwa kuti Mulungu adzachita chinthu chinachake. Ndiye iwo azolowera kwambiri zonyansa, ndipo amadyetsedwa nyansi, mpaka iwe. . . chabwino, sungalankhule nawo iwo, iwo sangawamvere basi Iwo, ndizo zonse. Galu. . . Baibulo linati, "Monga galu amabwerera ku masanzi ake, ndi nkhumba ku thope lake, chomwechonso iwo akutero."

122 Akamvetsera Mawu, ndipo amabwerera nso ku thope lakale lomwe lija! Ndikuti, "Ah, Ndi kutengeka. Musakhulupirire chinthu ngati chimenecho."

123 Mulungu. . . nkhosa zikuchita zomwezo lero, izo zikuyenera kudalira pa chakudya cha Mawu. Izo sizidya chakudya chirichonse. Inu simungazipatse chakudya chachipembedzo, nkhosa zenizeni. Ayi! Ayi! Mukapita ndi kukawauza iwo, "Tsopano taonani, ife tonse tikhale amodzi. Tsopano, Yesu anapemphera kuti tonse tikhale 'amodzi.'" Inu mwangomva kumene chinthu chomwecho ku Tucson osati kale, masiku angapo apitawo, koma ndi bodza! Yesu sanapemphere konse. . . Kodi Iye anachita motani. . . Mungawapangitse bwanji Mawu kuti adzitsutse Okha, kudzitembenukira Iwoeni? Ndiye Mulungu sali woposa munthu wina aliyense.

124 Yesu anati, "Kodi awiri angayende bwanji limodzi pokhapokha atagwirizana?" Inu mungawatenge bwanji Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, ndi Akatolika, ndi kuwaponyera iwo onse pamodzi ndi kukhala amodzi? Inu mukhoza kukhala mmodzi pansi pa mutu wa munthu, koma Yesu anati, "Kuti akhale amodzi monganso—monga *Ine* ndi *Inu* tiri mmodzi." Tsopano, Iye akufuna ife tonse tikhale mmodzi mwa Iye amene ali Mawu! Ameni! Ndi zimenezotu, "Mmodzi ndi Atate." Ndipo Atate ndi Mwana, ndi yemweyo. Ndipo ndi Mawu yemweyo, Mawu akuwonetseredwa, akudziwonetsera Okha mu tsiku lino monga Iwo ankachitira mu tsiku lina lirilonselo, kuti inu mukhale amodzi.

125 Zindikirani, Iye anati, "Monga Atate anandituma Ine, Inenso ndikukutumani inu." Atate amene anamutuma Iye, anadzalowa mwa Iye kuti akawatsimikizire Mawu. Ndipo Yesu yemweyo amene amawatuma anthu Ake, amalowa mwa anthu amene Iye wawatumawo; ndikuti, "Ntchito zimene Ine ndikuchita,

inunso mudzazichita." Ndithudi, Iye anapemphera kuti ife tikhale amodzi; mmodzi ndi Iye, osati mmodzi ndi bungwe. Osati mmodzi wokhala ndi kachitidwe, koma mmodzi ndi Mulungu. Pakuti Mulungu mu Mawu Ake ndi Mmodzi, ndipo Yesu ndi Mulungu anali Mmodzi, ndipo inu ndi ine ndi Mawu tikuyenera kukhala mmodzi. Uko nkulondola. Ife tikuyenera kukhala mmodzi ogwirizana ndi Mawu. Osati zimene wina akunena, izi ziribe kutanthauzira kwamseri. Muziwatenga Iwo, chimene Iwo akunena, ndi kuwakhulupirira Iwo; ndipo Mulungu adzawatsimikizira Iwo, ndi kutsimikizira kuti Iwo ndi olondola. Inu mukuganiza kuti Iwo ndi a ophunzira okha, atengeni Mawu Ake a izo, mupite mukawayese kamodzi ndipo muwone. Inu mudzapeza kuti zidzagwira ntchito pa inu chimodzimodzi basi monga momwe Iye analonjezera. Inde, bwana!

126 Iwo sangadye nyansi, iwo akuyenera kukhala ndi chakudya cha nkhosa. Yohane Woyera 10 amafotokoza kuti, "Nkhosa zanga zimadziwa Liwu Langa." Ndipo ngati Iye ali Mawu, ndiye Iye ali ndi Liwu la mtundu wanji? "Nkhosa zanga zimadziwa Liwu Langa, alendo sizimawatsatira." Mukuona? Yesu anati, "Liwu lachilendo izo silidzalitsatira." Chotero, nkhosa Zake sizimatsatira liwu la mlendo. Izo sizingawatsatire iwo.

127 Aneneri, azibusa, ndi nkhosa, onse akuchitira umboni za kubwera.

128 Tsopano taonani Mulungu wosasintha mu madongosolo Ake osasintha a Mawu Ake lero. Tsopano tangoganizani maminiti pang'ono: Mawu osasintha.

129 Tsopano taonani! Ngati—ngati Mose akanabwera ndi uthenga wa Nowa, sukanagwira ntchito. Ngati Yohane M'batizi akanabwera ndi uthenga wa Mose sukanagwira ntchito. Ngati Yesu akanabwera ndi uthenga wa Mose kapena wa Nowa, iwo sukanagwira ntchito. Ndipo Wesley kubwera ndi uthenga wa Luther, sukanagwira ntchito. Ngati Pentekoste ikanabwera ndi uthenga wa Wesley, sukanagwira ntchito; ife tangomva kumene zimenezo zikuchitira umboni. Tsopano, Mulungu amangopitirira kumasuntha. Muzingopenya Mawu, inu muwona pamene ife tiri.

130 Ndiye nchifukwa chiyani kusakhale kulengeza koyamba kwa abusa...Ngati aneneri onsewa, amuna aakulu onsewa anali azibusa, ndiye nchifukwa chiyani Mulungu (Wosasinthayo) angasinthe njira Yake pomwe pano, ndi kuwubweretsa Iwo kwa a fioloje? Iwo anali azibusa. Kufika kwa Mwanawankhosa wangwiro, nsembe ya tchimo, kukuyenera kubwera kwa m'busa.

131 M'busa amazidziwa bwino nkhosa zake kuposa wina aliyense. Palibe amene amazidziwa nkhosa monga m'busa, iye amaphunzitsidwa zimenezo. Komanso ankadziwa mtundu wa chakudya chimene izo zingadye. Iwo...iye ankadziwa chimene nkhosa zingadye, ndipo iye amadziwa nkhosa zake ndi chimene

izo zimadya. A...mutaiwona nkhosa ikupita ku khola la nyansi ndi kuyamba kudya nyansi, inu mungati, "Mchotseni khwangwala ameneyo." Mukuona? Chotero Mulungu anadziwa komwe angatumize izo.

132 Tsopano tiyeni tiitane mmodzi wa aneneri opambana awubusa a Yehova, kuti titsimikizire kuti Mulungu anali mwa aneneri amenewa pansi pa chikopa cha nkhosa. Taonani tsopano. Ife tiitana, poyamba, Mose. Tiyeni timuyang'ane iye. Utumiki wake utiwonetsa ife Yehova mwa m'busa mneneri Wake. Tsopano, tingotenga mwinamwake mmodzi, ngati tingakhale ndi nthawi, kwa pafupifupi maminiti teni otsatirawa. Ife titenga awiri a iwo, koma mwinamwake uyu akhala wabwino.

133 Mose; Yehova akudziwonetsera Yekha apa, mwa m'busa mneneri uyu. Iye anapatsidwa mphatso zitatu zotsimikizira utumiki wake ndi kuyitanira akulu akulu a Israeli, ndi kwa Farao. Zindikirani m'busa-mneneri uyu, tsopano. Iye amawapatsa, nthawizonse, aneneri Ake, chizindikiro chauzimu, kuti akatsimikizire kuti anali Mulungu mwa iwo; pakuti sipangakhale kupezeka kwa Mulungu popanda zinthu zauzimu kuchitikapo. Yehova sanawonekere konse popanda chauzimu chikumutsatira Iye. Zimayenera kumatero. Chotero Iye nthawizonse ankadzitsimikizira Yekha kuti Iye amakhala ndi aneneri awa, potsimikizira chimene iwo ankanenera, ngati izo zinali molingana ndi Mawu Ake.

134 Tsopano, choyamba—chizindikiro choyamba chimene Iye anapereka kwa...mneneri-m'busa uyu (yang'anani), anasandutsa ndodo yake kukhala njoka.

135 Chachiwiri, dzanja lake linasanduka lakhate.

136 Chachitatu, kukatunga madzi kuchokera mu mtsinje wa Nailo ku Igupto, ndi kuwasandutsa iwo magazi.

137 Tsopano, Iye anamupatsa iye zizindikiro zitatu kuti akatsimikizire kwa Igupto, ndiponso kwa Israeli, kuti iye anali Mawu olankhulidwa ndi Mulungu.

138 Tsopano, kumbukirani, Mose anaitanidwira mu chirengedwe! Uko nkulondola. Anatenga mchenga ndipo anawuponyera iwo mmwamba, ndipo anati, "Utitiri ubwere," ndipo utitiri unabwera. Anati, "Ntchentche zibwere," ndipo ntchentche zinabwera. "Achule abwere," ndipo achule anabwera. Iye anabweretsa mu chirengedwe! Tsopano, munthu sangalenge, koma sanali munthu kuyamba ndi kuyamba. Anali Yehova mwa mneneri m'busa Wake! Ameni!

139 Taonani! Chizindikiro chachitatu chimene Iye anamupatsa sichinali chokhudzana ndi ntchito yake, komanso sichinali chokhudzana ndi umunthu wake; chizindikiro chake chachitatu. Zindikirani, zizindikiro ziwiri zoyambirira zinkakhudzana ndi iye, iyemwini ndi ntchito yake. Ndipo izo zinali zizindikiro ziwiri zokhazo zimene Baibulo limanena kuti "zinali ndi liwu."

Chizindikiro chinacho chinalibe liwu. Koma zizindikiro ziwiri zimene zinaperekedwa kuchokera kwa umunthu wake, ndi kwa anthu ake, zinali ndi mawu. Koma chizindikiro chachitatu, tsopano zindikirani, icho chinaperekedwa . . . chizindikiro, chizindikiro chachitatu, chinali chizindikiro cha imfa: madzi akusandulika kukhala magazi. Ngati anu—ngati anu—ngati magazi anu angasandulike kukhala madzi, ndiye kuti inu mukhoza kufa. Ndipo pamene pali magazi, magazi okhetsedwa, ndi chizindikiro cha imfa; momwemonso zinali kwa Farao. Chachitatu chinali choti awasandutse madzi amu Nailo kukhala magazi, anali woti asonyeze—kuti asonyeze Uthenga wake kwa Farao kuti Mulungu wathu ndi Mulungu wa pamwamba pa Nailo, pamwamba pa mulungu wa Nailo. Iye ndi Mulungu wa pa chirichonse, ndipo Iye abweretsa imfa ku fuko limenelo. Ndipo ndicho chimene chizindikiro cha magazicho chinali. Oh, mai! Chizindikiro cholunjika cha imfa: magazi!

140 Koma ziwiri zinazo zinali ndi mawu a uneneri. (Ine—ine—ine ndikukhulupirira kuti mukuwerenga tsopano, pakati pa mizere, chimene ine ndikunena.) Koma zizindikiro ziwiri zinazo zinali ndi maliwu a uneneri kwa Israeli zokhudzana ndi tsogolo lawo. (Tsopano kwa inu amene munali uko pa phiri posachedwapa, pamene mwala unaponyedwa mmwamba.)

141 Tsopano, ndi kupita . . . anali woti asinthe chirengedwe, kuti chidziwathandizira iwowo. Taonani msanamira, taonani serpenti, taonani Nyanja Yofiira, ndi chirichonse chimene Iye anachita, tsopano. Tayang'anani pa ndodo ya m'busayo ikupanga njira yoti iwo apitire. Ndodo ija imene inali mdzanja la m'busa, inalambalala chidutswa chirichonse cha fioloje ndi zinthu zonse zimene ansembe ananena, ndipo ndodo ya m'busa ija inawatsogolera iwo kupita kudutsa mu chinthu chirichonse chosatheka (kwa anthu). Pamene Farao ankayesera kumaganiza kuti "mathithi anaphulika mmapiri ndipo anadzaponyera madzi, kenako zinapangitsa kuti iwo asanduke kukhala magazi," kenako Mulungu anavumbitsa moto kuchokera kumwamba. Ndipo Iye anavumbitsa matalala kuchokera kumwamba, ndipo Iye—ndipo Iye anavumbitsa nsabwe pa dziko lapansi, ndi chirichonse.

142 Kodi Iye anachita chiyani? Ndi ndodo ya m'busayo, osati a—bukhu, osati lingaliro la wa fioloje, koma ndodo ya m'busa! Ife tibwera kwa zimenezo mu miniti; ndodo ya m'busa, Iye anachita izo. Osati a—bukhu la pemphero la chipembedzo, koma ndodo ya m'busa. Ndodo ya m'busa ikutsogolera nkhosa zake, kukonza njira pamene izo zimapita ku Mawu olonjezedwa mdzikolo. Ndi chinthu chokongola bwanji lero cha Ndodo ya M'busa, lero, ikutsogolera nkhosa Zake ku Dziko Lolonjezedwa; kulambalala fioloje yonse ndi china chirichonse cha mdziko lino, ndi zinthu za mdziko, ndi zipembedzo, chirichonse; kutsegula njira, ndi kutsimikizira Mawu Ake kuti ndi Choonadi; Ndodo ya M'busa

ikupita patsogolo.

143 Ndipo zindikirani, ndodo yomweyo ya m'busa imene inkatsogolera nkhosa. . .Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Iye ndithudi ankatsogolera nkhosa, anawapulumutsa iwo kuchokera ku Igupto ndi ndodo imeneyo mdzanja lake. Ife tikhoza kunena zochuluka zambiri za izi. Koma kuti tikhudze mfundo zikuluzikulu, iye anatsogolera nkhosa ndipo anatumiza chiweruzo chifukwa chowakana Iwo! Ndodo yomweyo imene inali mdalitso kwa mmodzi, inadzakhala themberero kwa enawo. Madzi omwewo (a kulalikira kwa Nowa) amene anamupulumutsa iye, anaweruza dziko lapansi. Ndodo yomweyo imene inatsogolera Israeli kupita ku dziko lolonjezedwa, inawatsutsa iwo amene anakana kutsatira mneneri m'busa. Izo nzoona, inadzakhala ndodo ya chiweruzo.

Chirengedwe; zindikirani momwe Mulungu amayankhulira mu chirengedwe Chake. Ngati ife tikanangokhala nayo nthawi. Ine ndinalemba cholemba pamenepo: Mulungu akuyankhula mu chirengedwe Chake. Tiribe nthawi yoti titsimikizire izo.

144 Koma podzatsimikizira mtsogolo, ndi njoka yamkuwa pa ndodo ya nkhosa ya m'busayo (kuti ankaikulunga njoka iyi, mchipululu), izi zikukamba za chitetezero choona chikubwerera matenda ndi tchimo.

145 Ndodo ija payokha inali itasandulika njoka pamaso pa Farao, ndipo Farao yemweyo anayesera kutsanzira ndi amatsenga. Ndipo chomwechonso Afarao amakono a lero akumatero, ndi odzipangitsa kukhulupirira, onyengezera achithupi a Uthenga, amayesera kutengera chinthu chomwecho osadziwa kumene icho chikuchokerako; ndi kuwuponyera Iwo mu chinachake cha chipembedzo, pamene Iwo ndi wosakhudzana ndi izo monga momwe mpweya umakhalira ukatsekeredwa. Ndithudi! Koma kuyesera kutsanzira, kupanga kutsanzira.

146 Koma, zindikirani, ndodo yomweyo ya m'busayo inadya njoka zinazo. Kodi njoka zimenezo zinapita kuti? Zinali ndodo pansi, ndipo panali ndodo imodzi yokha imene inatoledwapo. "Kumwamba ndi dziko lapansi zidzapita," anatero Yesu, "koma Mawu Anga sadzapita." Amayankhula za chitetezero chenicheni chimene chikubwera cha tchimo.

147 Komanso, tsogolo la Israeli linapereka. . .ndipo uko kumene ndimayankhula za Israeli, tsopano mtsogolo. . .Kumeneko iwo anapatsidwa chiwombolo ku ukapolo wa imfa ndi mneneri-m'busa. Iwo anatulutsidwa mu ukapolo ndi mneneri-m'busa wokhala ndi ndodo. Mukuona? Izo zinkayankhula za Muomboli wa mtsogolo wa Israeli, kuchokera ku imfa ndi gehena, ndi M'busa-Mneneri amene titamukambe.

148 Tsopano, kwa onse amene. . .onse monga ife tikudziwira Israeli, sanawalandire Mawu a mneneri-m'busa, Israeli

yense sanawalandire Iwo. Tsopano, zindikirani, iwo anali kudandaula. "Oh," pamene iwo ankachita zozizwitsa, "iye anali munthu wamkulu," koma pamene zinafika ku Uthenga wake, "izo zinali zosiyana." Zizindikiro zazikulu zonse zimatsatira uthenga watsopano umene ukubwera. Tikudziwa zimenezo. Mu chipululu iwo anadandaula, mu chipululu, ndipo anamwalira m'masauzande. Kunena moona, kunalibeko awiri okha mwa iwo amene anapitako amene anapulumutsidwa pa thuu millioni ndi theka, awiri pa thuu millioni ndi theka.

149 Inu mukuti, "Icho. . .Chinachitika ndi chiyani kwa iwo?" Iwo anapita Kwamuyaya.

150 "Onse a iwo, M'bale Branham?" Yesu ananena chomwecho.

151 Iwo anati, "Makolo athu anadya Manna mchipululu, ndipo anamwa kuchokera mu Thanthwe."

152 Ndipo Iye. . .Yesu anati, "Ndipo iwo ali, mmodzi aliyense wa iwo, anafa," analekanitsidwa Mwamuyaya, mwaona, mmodzi aliyense.

153 Zindikirani iwo ankadandaula za njira yoperekedwa ndi Mulungu, ndi chifukwa chimene iwo anafera. (Tsopano, mwatcheru, musaphonye ndemanga zochepa zomalizirazi.) Iwo anadandaula! Chimene chinawapangitsa iwo kufera mchipululu, ankadandaula za njira yoperekedwa ndi Mulungu: ndi Uthenga wa munthu mmodzi, mneneri, utsogoleri wa munthu mmodzi. Ndiuzeni ine pamene Mulungu anayamba wagwiritsapo ntchito gulu kuti lizitsogolera. Simudzazipeza zimenezo mu Baibulo. Munthu mmodzi, iwo. . .Mawu anadza kwa Mose!

154 Korah; ife tonse tikudziwa kuti iye—anadzitolera yekha ndipo anadandaula za Mulungu kuti sanachite bwino, pochita chinthu chonga chimenecho, pomupanga munthu mmodzi kukhala ndi Uthenga. Iye anati, "Ndife tonse oyera. Bwanji osakhala ndi chipembedzo? Ndipo bwanji osakhala ndi. . . kukhazikitsa *ichi*, ndi kuchita *ichi*, ndi kuchita *icho*?"

155 Mulungu anamuuza Mose, "Dzipatule wekha kwa iye, Ine zandikwana zimenezo." Ndipo kumbukirani, Yuda akuyankhula chinthu chomwecho, mmasiku otsiriza. Uko nkulondola, "Iwo anawononongeka nzoyankhula zopanda pake za Korah." Ifenso tikudziwa chimene chinachitika kwa Korah ndi—ndi ena onsewo amene anawakaikira Mawu a Mulungu ndi nzeru za Mulungu za utsogoleri wa munthu mmodzi uja: mmodzi aliyense wa iwo anawononongeka.

156 Tsopano, ife timuzindikira Mulungu mwa m'busa-mneneri, akuwonetsera madongosolo Ake a mtsogolo mu liwu lachizindikiro lotsatira. Tsopano, taonani. Tikuziwona izo *pamenepo,* tsopano tiyeni tiwone mu chizindikiro chotsatirachi.

157 Tsopano, zindikirani, iye anatumizidwa kwa abale ake mu ukapolo, pansi pa nsinga, ndi Uthenga wa chiwombolo, ndi chizindikiro choperekedwa ndi Mulungu kuti akatsimikizire zonena Zake. Israeli anatsatira Uthenga wake, iwo anawukhulupirira Iwo, aliyense wa iwo, koma mu nthawi ya kumadzulo. . .Iwo anatsatira zozizwitsa zake, koma mu nthawi ya kumadzulo pamene iwo. . .iye anapereka Uthenga wake, "Zinali zosiyana." Onse amene sanakhulupirire Uthenga umenewo, anafa. Uko nkulondola. Uthengawo unali chiyani? Uthengawo unali wa chiweruzo chimene chinkabwera. Madzulo, nthawi ya kumadzulo, Mulungu anatuluka pa msasa wa Israeli kuti akafufuze ngati anthuwo anali atakhulupirira Uthenga Wake wa m'busa-mneneri; ndipo onse amene anali asanawukhulupirire Iwo, anawonongeka.

158 Tsopano zindikirani, ife tizibweretsa izo kwa M'busa Wamkulu mu mphindi pang'ono chabe. Mukuona? Zindikirani utumiki wa M'busa-Mneneri Wamkulu. Mwa zozizwitsa Zake, mpingo uliwonse unatseguka ndipo ukanamulandira Iye. Iwo ankafuna kuti odwala awo achiritsidwe. Ankafuna kuchita zinthu zazikulu. Kutchuka kwake kunali kwakukulu. Koma pamene nthawi ya kumadzulo inadzafika, tsiku lina Iye atasandutsa madzi kukhala vinyo, ndipo anali atadyetsa masauzande, mkate, ndipo anali atachita zozizwitsa, Iye anayamba kukhala pansi ndi kuyankhula nawo. Ndipo Iye anati kwa iwo, "Ine ndi Atate Anga ndi mmodzi. Chifukwa chiyani inu mukuti, 'Tiwonetseni ife Atate'?"

159 "Oh, m'bale! Munthu uyu akudzipanga yekha wofanana ndi Mulungu?" Izi zinali zowonjeza kwambiri pa kuganiza kwawo kwa chipembedzo. Koma icho chinali Choonadi, Iye anali! Mukuona? Koma pamene iwo anatero, ambiri sanamutsatire Iye.

160 Kenako Iye anatembenuka ndipo anati, "Pokhapokha mutadya Thupi la Mwana wa munthu, ndi kumwa Magazi Ake, inu mulibe Moyo mwa inu."

161 Tsopano, mukuganiza kuti munthu wanzeru, waluntha angaganize chiyani? Ine ndikulingalira ansembe amene anali atakhala ndi Iye mu kachisi anali kwambiri—ankachita manyazi kwambiri ndi—kuti amuitanire Iye kumeneko. "Kuganiza kuti munthu angaimirire ndi kunena chinthu ngati chimenecho, 'Pokhapokha anthu inu mutadya Thupi Langa, ndi kumwa Magazi Anga.'" Anati, "Uyu ndi wokudya anthu, mwaona, 'Idyani Thupi Langa ndi kumwa . . .' Bwanji, ndi wokudya anthu. Inu anthu oganiza bwino mu. . .inu muchoke kwa wamisala ngati ameneyo."

162 Iye sanawafotokoze Iwo, Iye anangowanena Iwo! Iye anachita zimenezo kuti awapunthwitse iwo, kuti alekanitse nkhosa Zake kwa mbuzi. Iye anachita zimenezo kuti awataye iwo. Ndipo zitatero panalibe amene ankafuna kuti agwirizane

ndi Iye. Iwo analibe mgwirizano kuyambira pamenepo. Mukuona?

163 Zindikirani, pa nthawi ya kumadzulo, Mulungu anatulukira kudutsa mmisasa ndipo anawona amene anakhulupirira. Ndipo Iye anachita chinthu chomwecho mmasiku a M'busa Wamkulu. Zindikirani utumiki wa M'busa Mneneri Wamkulu, koma zindikirani ichi, kwa okhulupirira a Uthenga Wake, koma osati . . . Uthenga wakumadzulo uwu, sangawukhulupirire Iwo. Iwo sangakhulupirire kuti Iye anali Mulungu. Iwo ankafuna kumupanga Iye kukhala munthu wabwino. Iwo ankafuna kumupanga Iye mneneri. Iye anali munthu wabwino, ndipo Iye anali Mneneri, koma Iye anali woposa zimenezo. Ndicho chiphunzitso chawamba lero, kuti "Iye ndi munthu wabwino basi, iye anali mneneri." Iye sanali wochepera pa Emmanuele! Iye anali Mulungu akuwonetseredwa mwa Yesu Khristu Mwana Wake, kumupanga Iye ndi Atate mmodzi. Ndizo zonse zimene Iye akanakhala.

164 Zakariya 14:7, ine ndikhoza kunena ichi, akuyankhula za Kuwala kwa kumadzulo ndi Uthenga kenanso pa nthawi yakumapeto. Kodi inu munazindikira zimenezo? Ambiri omwe anamutsatira Mose, anawona Lawi la Moto limene linamuzindikiritsa iye pa Phiri la Sinai. Iye anali atachitira umboni, ndipo anayankhula za Lawi la Moto ili mu chitsamba ndipo linamuuza iye Uthenga uwu, ambiri a iwo sanawukhulupirire Iwo. Koma onse amene anamutsatira iye kuchokera ku Igupto (anatuluka mdzikolo ndipo anakawoloka nyanja ya kulekana, ndipo anapita mchipululu), anawona Lawi la Moto lomwelo (limene iye ankalikamba) kutsimikizira kuti mneneri-m'busayo anali m'busa wa nkhosa. Iwo anawuwona Iwo, ndipo ambiri a iwo sanawukhulupiririrebe Iwo atawuwona Iwo.

165 Zindikirani momwe, kenanso, Mulungu wosasintha, M'busa-Mneneri Wamkulu, anawatengera iwo amene anakhala ndi Iye ndi utumiki Wake ku Phiri la Azitona; M'busa-Mneneri Wamkulu, Iye amene tikumukambayu, Yesu. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . ? . . . ndipo anawamva Atate (Lawi la Moto lomwelo) akumutsimikizira Iye, amene anamutsimikizira Mose.

166 Mulungu yemweyo amene Mose ankamukamba, anabwera pa Mose ndipo anatsimikizira mwa Lawi la Moto kuti Iye anali Yehova amene ankamutsogolera Mose. Mulungu anali mwa m'busa-mneneri Wake.

167 Apa Iye akumutenga M'busa-Mneneri wina, Mneneri Wamkulu, Nkhosa Yeniyeni, Yesu, ndipo akutenga kusankha kwa amuna atatu, ndipo akuwatengera iwo pamwamba pa Phiri la Azitona, ndipo pamenepo anakamutsimikizira Yesu. Ndipo ngakhale kudzichotsapo Iyemwini kwa anthu ena onsewo, anati,

"Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa, mvereni inu Iye!" Ndipo pamene iwo anayang'ana mmwamba, iwo sanamuwone munthu koma Yesu yekha. Uko nkulondola. Iye anali Ameneyo. Tsopano, izo zikukhazikitsa zimenezo, monga mmene ine ndikuwonera. Mukuona?

168 [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . ? . . . [Malo opanda kanthu pa tepi.] . . . ? . . . nkhope. Mose anali pamaso pa Shekinah pa Phiri la Sinai. Zinasintha nkhope yake. Pamene ankatsika pansi, iye ankayenera kuti—ayike chophimba pa nkhope yake, mneneri-m'busa Mose; amene Yehova anali mmenemo, mwa kagawo, kagawo chabe, nkhope yake. Iye anali ali ndi Mawu mkamwa mwake.

169 Koma zindikirani pamene M'busa Wamkulu anali pamaso pa Shekinah. Kodi izo zinachita chiyani? Izo zinasintha nkhope Yake yonse. Iye sanangokhala gawo la Mulungu, Iye anali zonse za Mulungu! Iye anali Emanuele.

Chifukwa chiyani ankayenera kukhala abusa?

170 Taonani! Mwaona, tsopano, Mulungu Wamphamvuzonse akuyendayenda . . . akudziwonetsera Iyemwini, kani, mwa Mose m'busa-mneneri. Taonani momwe Mulungu anazidziwitsira Yekha. (Iyi ndi ndemanga yanga yomaliza.) Muwoneni iye, atayima wodzodzedwa pamaso pa Lawi la Moto! Panalibe wina aliyense paphiripo koma Mose ndi Yehova. Ameni! *Ameni* amatanthauza "zikhale chomwecho."

171 Penyani! "Ika dzanja lako pachifuwa pako!" Koma, penyani chizindikiro chachiwiri ichi ndi liwu. "Ika dzanja lako mchifuwa." Ife tiribe chifukwa choti tikhulupirire kuti Mose anali wa dzanja lamanzere, chotero iye akuyenera kuti ayike dzanja lake lamanja mchifuwa mwake, chifukwa anthu ambiri amakhala a dzanja lamanja. Iye anayika dzanja lake lamanja . . . Tsopano penyani! Ndi chithunzi bwanji chimene ife tikuchiwona apa, cha Yehova mwa Mose m'busa-mneneri! Mose akuyimira Mulungu, chifukwa Mulungu anali mwa Mose. Muoneni iye akuyika lake . . . "Dzanja mchifuwa chako." Ndi chizindikiro chotani!

172 Tsopano, apo iye wayima, atagwirizira dzanja lake lamanja pamtima pake (ataimirira monga *chonchi*) kumene zinsinsi zobisika za chiwombolo zinali zitabisika kuyambira pa maziko a dziko lapansi. Apa pali chifukwa chimene anali abusa. Yesu ndi dzanja lamanja la Mulungu, ife tonse timadziwa. Pamenepo pali Mose akumuwonetsera Iye ndendende. Iye anasungira zinsinsi za Atate, ndipo waziwonetsera izo kwa ife. Zindikirani, tamuoneni iye akukoka kuchokera mchifuwa mwake dzanja lake lamanja lokanthidwa ndi khate lakupha. Zinkawonetsera chimene Mulungu akanadzachita ndi Dzanja Lake Lamanja. Zindikirani, khate liribe mankhwala. Zindikirani, kenanso, ilo silinali khate wamba, linali mu gawo lake lotsiriza, loyera ngati

chipale; dzanja lake linakanthidwa ndi chinthu chowopsya. Momwe Mose ayenera kuti anamvererera pamene anatulutsa dzanja lake lamanja pamtima pake, kulichotsa mchifuwa mwake, ndipo dzanja lake linakanthidwa ndi khate! Khate limaimira tchimo, losachiritsika, ndipo makamaka mu gawo lake la kumapeto.

173 Ndipo, abale, pamenepo ndi pamene dziko linali pamene Mulungu anachotsa Dzanja Lake Lamanja mu chifuwa Mwake! Dziko linakanthidwa ndi khate lakupha, ndipo popanda mankhwala ake nkomwe. Zirinso chomwecho usikuuno, chifukwa iwo sangalandire mankhwala. Mankhwala anapangidwa pa Kalvare, koma anthu amafuna kutenga mankhwala opangidwa ndi anthu mmalo mwa mankhwala a Mulungu a tchimo.

174 Zindikirani ilo silimabwera pang'onopang'ono, monga khate limachitira, koma zonse mwakamodzi! Pamene iye anatulutsa dzanja lake, ilo linakanthidwa, ilo linali lodzadza ndi khate. Zindikirani chimene Mulungu ananena, "Tsopano, simudzasunthira pang'onopang'ono mu tchimo; koma tsiku limene mudzadye, tsiku limenelo inu mudzafa." Ndipo uko nkulondola, "Tsiku limene mudzadye za iwo."

175 Zindikirani, anali mneneri m'busa amene anadzikantha yekha. Iye anatenga, mwa lamulo la Mulungu, ndipo anadzayika dzanja lake lomwe mchifuwa mwake, ndipo analitulutsa ilo litagwidwa ndi khate. Mneneri-m'busa anachita zimenezo yekha. Ndipo Mneneri-M'busa Wamkulu, Yesu, anachita izo Yekha, "Ine ndidzawuyika moyo Wanga pansi, palibe amene adzawuchotse iwo kwa Ine." Iye anali M'busa Wamkulu, Mneneri-M'busa Wamkulu, "Palibe munthu adzawuchotse iwo kwa Ine, ndimazichita izo Ndekha." Zindikirani ilo silinabwere pang'onopang'ono, linabwera mu miniti. M'busa Wamkulu, Iyemwini, anachotsa kulakwa kwathu ndipo anadzikantha Yekha, anatenga machimo athu ndipo anadzawayika iwo pa Iyemwini. Nzosadabwitsa wandakatulo analemba:

> Pakati pa miyala yosweka ndi mlengalenga mwamdima,
> Mpulumutsi wanga anaweramitsa mutu Wake ndipo anafa;
> Chophimba chotseguka chinaulula njira
> Ku chisangalalo cha Kumwamba ndi tsiku losatha.

176 Chinsinsi chimenecho chinali chiri pa chifuwa cha Mulungu zaka zonsezi, chophimbidwa ndi dzanja Lake lamanja, Yesu. M'busa Wamkulu anadzitengera pa Iyemwini kulakwa kwathu chifukwa cha ife. Yesaya 53:6, anati, "Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu. Iye anatunduzidwa chifukwa cha kusaweruzika kwathu. Chilango cha mtendere wathu chinali

pa Iye. Ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tachiritsidwa." Chinsinsi cha machiritso a Mulungu chagona mu chifuwa mwa Yesu Khristu, kapena Mulungu, Iye anali kudzanja lamanja la Mulungu, ndiyo Nkhosa yokhayo imene inagwira chinsinsi chake mu chifuwa Mwake. Ndicho chifukwa chimene mithunzi ya Icho imayenera nthawizonse kukhala nkhosa! Woyamba unali nkhosa, wotsiriza unali Nkhosa. Ndi chifukwa chake Iyo inkayenera kubwera kwa m'busa, kuti adziwe momwe angasamalire Nkhosa zake. Inu mukumvetsa Izo? Zindikirani, "Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu, chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye."

177 Zindikirani, ilo linabwera mwachangu; ndipo linachoka mwachangu, posakhalitsa dzanja lamanja linatulutsidwa mu chifuwa kachiwiri. Nthenda yowopsyayo inali itapita, pamene iye anatulutsa ilo kachiwiri. Ndipo pamene M'busa Wamkulu, Mneneri-Nkhosa, pamene Iye anati. . .Pa mtanda wa Kalvare, pamene Iye analipira chilango cha tchimo chifukwa cha ife tonse, Iye anati, "Kwatha." Tchimo linali litatha, chilango chinalipiridwa, ngongole inathetsedwa! Izo sizinatenge chaka, kapena pomalizira pake kulowa mmasiku a wokonzanso wina kapena chinachake, izo zinamalizika pomwepo!

178 Tchimo linabwera mkamphindi, pa kulakwira Lamulo la Mulungu, pakuswa Mawu amodzi. Usikuuno, abale anga, moyo wanu uli pamwamba pa gehena pa unyolo. Ndipo unyolo umenewo si kuphunzitsa kwina kwa fioloje ya ku seminare, unyolo umenewo si chipembedzo chinachake kapena kachikhulupiriro kena kamene mukukhala nako, unyolo umenewo ndi Mawu a Mulungu! Yesu anawupatsa mtundu wa anthu Mawu Ake kuti azikhala nawo moyo, ndipo Eva anangoswa polumikizira pamodzi papang'ono pa Iwo. Ndipo a. . .unyolo uliwonse sumakhala wamphamvu kuposa polumikizira pake pofowoketsetsa. Pamene muwachotsa Mawu amodzi. . .Icho chinali choyamba cha Bukhu.

Yesu anadzabwera pakati pa Bukhu, ndipo anati, "Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu." Pamenepo panali pakati pa Bukhu.

Kumapeto kwa Bukhu, Iye anati, "Aliyense amene adzatenge Mawu amodzi (kuwamasulira molakwika Mawu amodzi), kuwachotsa Mawu amodzi Umu, Ine ndidzachotsa gawo lake mu Bukhu la Moyo." Inu mukudutsa gehena, mutapachikika pa Mawu a Mulungu. Musalole kuti winawake afinyire chinachake mwa inu chimene sichiri PAKUTI ATERO AMBUYE!

179 Oh, ine ndikuwona. . .Chabwino, iwo amati, "Ndithudi, zonse ife tachita. Zonse ife tachita!" Icho ndi chimene mwinamwake ansembe aakulu ndi iwo ankaganiza mmasiku a

M'busa Wamkulu. Ndi chimene Eva ankaganiza. Ndi chimene Satana anamuwuza iye, "Ndithudi Mulungu sadzatero." Koma Iye anatero, chifukwa Iye anati Iye akanadzatero. Ndipo ndicho chifukwa chimene Iye achitenso izo lero.

180 Nzosadabwitsa, monga Iye anati, "Monga izo zinali mmasiku a Nowa, mmene miyoyo eyiti inapulumutsidwa, ndi madzi, chomwechonso zidzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu." Mwaona, apang'ono kwambiri, "Pakuti khwalala ndi chipata, ndipo yopapatiza ndi njira imene imatsogolera ku Moyo, ndipo apang'ono adzakhalapo amene adzayipeze Iyo." Uko nkulondola. "Chifukwa yotambalala ndi njira imene imatsogolera ku chiwonongeko, ambiri adzapita kumeneko."

181 Pamene M'busa Wamkulu anakanthidwa, Nkhosa Yaikulu-Mneneri, pamene Iye anakanthidwa kumbuyo uko, Iye anati, "Kwatha!" Ndipo miniti imeneyo, mwamsanga M'busa atangokanthidwa, zinali zitatha. Tchimo linathetsedwa, panalibenso tchimo. Iwo anali oyera, chilango chinalipiridwa. Okhulupirira amene maina awo analembedwa mu Bukhu la Moyo, okonzedweratu kuchokera ku maziko a dziko lapansi, zinatha miniti yomweyo imene Yesu anati kwatha. Iye, M'busa Wamkulu ameneyo, anali atabwerera nkhosa Zake. Zinali zitatha, dzanja lamanja la Mulungu linachotsedwa mu chifuwa Mwake, litakanthidwa. Kenako pa Isitala Iye analibweza ilo (ameni), analiyikanso mu chifuwa Mwake, ndipo analitambasulira ilo kudzafika kwa inu ndi ine, mmawonekedwe a Mawu Ake, kuti adzatiwombole ife kubwerera ku munda wapachiyambi kumene tchimo linatichotsako ife. Chinsinsi chobisika cha mtima Wake waukulu chinaululidwa ndi Mneneri-M'busa. Icho chinaululidwa ndi M'busa, Mneneri-M'busa.

182 Nzosadabwitsa mapiri analumpha ndipo anafuula pa tsiku limenelo. Nzosadabwitsa kuti dzuwa linabisa nkhope yake ndipo linafuulira chisangalalo. Nzosadabwitsa kuti chirengedwe chonse chinamasulidwa; mphepo inagwedeza mitengo mpaka inagwedezeka ndi kugwedezeka, ndi kusangalala, ndi kulumpha. Iwo anamuwona Mneneri-M'busa, pa phiri, akuwombola dzina lirilonse pa Bukhu la Moyo. Ndipo izo zinawona kuti chikhalidwe chawo chomwe chinawomboledwa! Izo zinafuula, ndipo zinalumpha. Ndipo dziko lapansi linalowa mu chivomezi. Ndipo mapiri anang'ambika, ndipo miyala inagwa. Ndipo dzuwa linalowa. Ndipo—ndipo chirichonse chinachitika. Monga msonkhano uliwonse, pamene M'busa awulula kwa inu kuti "kwatha!" Apo. . .

183 Ine ndawonapo zolumpha, ndi zachisangalalo, koma panalibe amene anavulala. Mapiri anatumphuka, ndipo iwo. . .dzuwa linakalowa, ndipo chirichonse chinachitika, koma panalibe amene anavulala. Ndipo ine ndawonapo misonkhano kumene mphamvu ya Mulungu inaululidwa kwa anthu kuti iwo "anali amfulu kwa dziko ndi zinthu

za mdziko," ndipo chimwemwe cha Ambuye nkudzadza mwa osonkhano. Iwo anaimirira ndi kufuula, ndi kulira, ndi kufuula pamwamba pa mawu awo, chifukwa cha ulemelero wa Mulungu. Ine sindinawonepo chirichonse chopanda dongosolo, iwo nthawizonse anali momwemo mu dongosolo; chifukwa anali atazindikira kuti, dzina lawo limene linali litalembedwa pa Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa maziko a dziko asanakhazikitsidwe. Mneneri-M'busa wamkulu anali atawabweretsera iwo Uthenga, ndipo iwo anapulumutsidwa, Mneneri-M'busa. Ziribe kanthu chimene magulu ena azipembedzo ankanena za Iwo, iwo ankadziwa chimene chinachitika. Basi monga abusa aja anachitira kumbuyo uko, iwo ankadziwa chimene chinachitika.

184 Palibe munthu amene amakhala ndi ufulu wolowa pagome lopatulika kuti azilalikira Mawu mpaka iye atachita monga momwe Mose anachitira, kukumana ndi Mulungu, iyemwini, pamaziko amene palibepo wa fioloje amene angamafotokoze Iwo mophotchola. Mose anali pamenepo! Ziribe kanthu momwe amthenga aku Israeli anati, "oh, zinali zamkutu, iwe ukungoganizira kuti unawona ichi; ndi zamkutu," inu simukanakhoza kuchotsa Zimenezo kwa iye, iye ankadziwa! Anali kumeneko! Iye anali amene zinamuchitikira! Ndipo palibe munthu wa—digiri ya fioloje kapena digiri ina ya udokotala amene ali ndi ufulu woyima kumbuyo kwa guwa, kumadzinenera Uthenga wa Yesu Khristu, mpaka atakumana kaye ndi Mulungu maso ndi maso mu Lawi la Moto. Iye alibe ufulu wodzitcha yekha mthenga, chifukwa a fioloje onse mdziko sangakhoze kuzifotokoza Izo mozichotsa kwa inu. Izo zinachitika kwa inu! Inu munali kumeneko, inu mukudziwa za Izo. Kusamala chimene wina aliyense anganene, kapena mochuluka momwe iwo anganene, "masiku anapita, izo siziri chomwecho," iwe. . . izo zinakuchitikira iwe, ndipo ndi molingana ndi Mawu.

185 Inde, ndi chifukwa chimene Mose anadziwira kuti Liwu ili limene linayankhula kwa iye, linali Liwu la Mawu. Iye ankadziwa kuti Mulungu anali atamuuza Abrahamu, "Mbewu yako idzakayenda ulendo kwa zaka foro handirede, koma Ine ndidzakawawombolako iwo." Ndipo iye ankadziwa kuti zaka foro handirede zinali zitatha ndipo iye anayitanidwa kuti akachite izo.

186 Amuna ndi akazi, Mulungu analonjeza mmasiku otsiriza ano kuti Iye adzatsanulira Mzimu Wake pa thupi lonse. Iye analonjeza kuti Iye adzatumiza Ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo Iye adzaitana Mkwatibwi wopanda banga kapena khwinya. Iye analonjeza kuti adzachita zimenezo, Iye adzachita zimenezo. Musawamvere azibusa aganyu awa, adzakusocheretsani inu. Mzimu Woyera ndi M'busa woti azikudyetsani inu chakudya cha nkhosa kuchokera ku Mawu awa. Izo nthawizonse zimabwera ndi M'busa. Iye ndi M'busa

wathu. Mumvereni Iye, inu ndi nkhosa za khola Lake; ngati inu muli, inu mumamvera Liwu Lake. Osati chimene wina akunena, inu mumamvera chimene Iye akunena. Liwu lachilendo, inu simumadziwa kanthu za ilo.

187 Oh, mai, mvetserani kwa m'busa-mneneri wamphamvu kenanso, akuwatanthauzira ndi kuwadziwitsa kwa iwo, Yohane (pamene iye anayima mu mtsinje wa Yordani), taonani chimene iye ananena (anali atayima pamenepo, akulalikira), iye anati, "Ora likubwera . . . "

188 Zindikirani, Yohane anali mwana wamwamuna wa wansembe. Iwo nthawizonse ankatsatira—mzere wa abambo awo, umo ndi momwe tinapezera mayina athu. Mwa chirichonse chimene iwo ankachita, iwo amawatcha iwo chimenecho. Ndipo Yohane ankayenera kudzakhala wansembe monga abambo ake.

189 Ndipo, inu mukudziwa, amayi ake, pamene iwo anali oyembekezera, Mngelo wa Ambuye atakumana ndi abambo ake Zakariya, ndipo anapita kunyumba kwa Elizabeti, ndipo iye anali kale ndi miyezi sikisi . . . kuti akhale mayi. Koma iye analibe moyo, anali ndi mantha chifukwa mwanayo anali asanasuntheko. Ndi zachilendo.

190 Ndipo Mzimu Woyera, Mngelo wa Ambuye anawonekera kwa Mariya, ndipo anamuuza iye kuti iye "adzakhala ndi mwana, osamudziwa mwamuna," ndipo anamuuza iye za momwe Elizabeti analiri.

191 Iye anakwera mmapiri a Yudeya, kukamuuza Elizabeti. Ndipo atakumana ndi Elizabeti, anamuuza iye kuti "adzakhala mayi." Ndipo samamvetsa zimenezo, "osamudziwa mwamuna." Koma iye anati, "Mzimu Woyera unandiphimba, ndipo unanena kuti chinthu Choyera ichi chimene chidzabadwa mwa ine chidzatchedwa 'Mwana wa Mulungu,' ndipo Ine ndidzamutcha Dzina Lake 'Yesu.'" Ndipo nthawi yoyamba imene dzina loti Yesu linayankhulidwapo pa mlomo wa munthu, mwana wakhanda wakufa, mmimba mwa amayi ake, anadumpha ndi chisangalalo ndipo anafuula; ndipo anadumpha mmimba mwa amayi, ndipo anali asanalandire moyo.

192 Dzina la Yesu Khristu linayankhula moyo kukhala mwa khanda lakufa. Kodi Icho chikuyenera kuchita chiyani mu mpingo umene umadzinenera kuti ndi wobadwa mwatsopano?

193 Ndipo timakhala owawasa ngati mabampu pa chipwete, ndi kumazisiya zinthu zoterezo kumapitirira. Ndipo kumawopa kudzuka ndi kuchitira umboni zomwe mukukhulupirira, ndi kutsutsa zamkutu zonsezi, kumupanga Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndi nthawi ya Khrisimasi, tulukaniko kwa ma Santa Claus ndi zinthu, mutalikirane ndi zamkutu za malondazi. Ndi pati munamvapo za Santa Claus mu Baibulo? Ndi nthano za Chiroma, palibepo chirichonse kwa izo nkomwe, palibepo chinthu choterocho.

Musamawaphunzitse ana anu zamkutu ngati zimenezo. Pamene tsiku lina inu mudzayenera kuti mumuuze iye kuti iyo inali nkhani yakhungu, ndiye kuti munamunamiza mwana wanuyo. Ndipo izo zidzavulaza umboni wanu wokhudza Yesu Khristu, iye adzati, "Mwinamwake Icho ndi chinthu chomwecho." Muyikenipo Yesu Khristu M'busa-mneneri Wamkulu abwerere ku Khrisimasi kumene Iye akuyenera kukhalako.

194 Zindikirani, mvetserani kwa mneneri uyu, Yohane, pamene iye wayima pamenepo. Ife tonse tikudziwa kuti iye anali m'busa-mneneri wamkulu. Tsopano, iye anali ndi uthenga, Mngeloyo ankadziwa kuti iye akufuna kuti amudziwitse Yesu.

195 Tsopano, sakanatha kupita ku seminare ina. Iwo akanati, "Tsopano, inu mukudziwa kuti Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti* ndi munthu woti atenge malowo tsopano. Inu mukuyenera kumudziwitsa iye. Ndipo inu mukudziwa zimenezo basi . . ." Mwaona, iye sakanatha kusakanikirana ndi munthu.

196 Pa usinkhu wa zaka naini, timauzidwa, anapita ku chipululu kukakonzekera pamaso pa Mulungu. Uko ndi kumene abusa amachokerako. Zindikirani uthenga wake sunali ngati wa fioloje, wokhala ndi mawu ena aakulu, ofufuma a mlingo winawake. Iye anati, "Oh, inu kam'badwo ka njoka." Kumamuwuza munthu wachipembedzo, "Inu gulu la njoka." Ndi zimene iye anakaziwona mchipululu, ankawona njoka. Chinthu chotsikitsitsa chimene iye anachipezako chinali njoka, ndipo iye anawatcha ansembe amenewo ndi atsogoleri ndi afioloje a tsiku limenelo, "Gulu la njoka!" Anati, "Ndani wakuchenjezani inu ku mkwiyo uli nkudza? Musayambe kunena, 'Ndife a *ichi*, ndipo ndife a *icho*,' pakuti ndinena kwa inu kuti Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu." Miyala, zimene iye ankaziwona mchipululu. "Komanso, nkhwangwa yayikidwa pa muzu wa mtengo." Ndi zimene iye anakhala akuziwona: njoka, mitengo, chipululu. Ndipo, mwaona, umenewo unali uthenga wake. Iye sankawadziwa mawu aakulu ofufuma a dokotala wina wamkulu wa umulungu (wokhoza kuwafotokoza Iwo onse mophotchola), iye ankangolalikira ndendende mzere wa chirengedwe.

197 Ndi chimene ife tikuwonetsa pano: ndodo ya m'busa, m'busa, nkhosa, mzere wachirengedwe.

198 Kodi iye anachita chiyani? Iye anali ndi chinthu chachikulu choti achite, iye anali mmodzi amene akanadzamudziwa Mesiya. Iye anati, "Ndikuti, 'Iye waima pano pakati panu tsopano. Ndipo inu simukumudziwa Iye, chifukwa fioloje yanu yakumangiririrani kwambiri, simukudziwa pamene inu muli.'"

199 Tsiku lina Yesu anabwera akutulukira, iye anati, "Taonani, apo pakubwera Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo la dziko lapansi." Mwanawankhosa! Aleluya! Chitetezero chenicheni! Apo pakubwera chimene nkhosa

iliyonse yochokera mmunda wa Edeni kumatsika inkaimira, Munthu wamba akuyenda kumapita kumtsinje.

200 Iwo anati, "Yohane, iwe wadziwa Izo bwanji? Ine sindinawone chinthu chimodzi chosiyana."

201 "Koma ndikuchitira umboni, ndinawona Mzimu wa Mulungu ukutsika ngati nkhunda, ndipo Liwu likuti, 'Uyu ndi Mwana Wanga Wokondedwa mwa Iye ndikondwera kukhalamo.'"

202 Taonani Nkhunda ndi Mwanawankhosa. Mukuona? Eya. Bwanji zikanakhala a. . . bwanji zikanakhala kuti chinali chinachake. . . Bwanji ngati ikanakhala nkhandwe itayima pamenepo? Chabwino, Mwanawankhosa ameneyo sakanapita pa. . . kapena Nkhunda ija. . . Mulungu anadziyimira Yekha ndi nkhunda, yofatsitsitsa kwambiri pa mbalame zonse za mlengalenga; Mwana Wake ndi nkhosa, yofatsa kwambiri pa nyama zonse pa dziko lapansi. Mwaona, mbalame yoyera ya kumwamba, osati khwangwala; osati mphamba, koma nkhunda. Osati nkhumba, koma mwanawankhosa. Chikhalidwe china chirichonse sichikanagwirizana limodzi.

203 Ndipo zindikirani pamene Nkhunda inadza pa Mwanawankhosa, Iyo inamutsogolera Iye. Osati momwe Iye akanachitira, koma momwe Atate akanati amutsogolere Iye. Umo ndi momwe mwanawankhosa weniweni aliri lero. O nkhosa za nthawi ya Khrisimasi, kodi simukudziwa kuti Mulungu amangotsogolera ndi Mawu Ake? Ndiwo ndodo Yake.

204 Zindikirani palibe chimene chinachitika, koma Yohane anati, "Ena onsewo sanaiwone Iyo, koma ndikuchitira umboni, 'Ine ndinaiwona Iyo.'" Kumuwonetsera: "Taonani, Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa machimo a dziko lapansi."

205 Ndiloleni tsopano ndikuwonetseni Uthenga wanga wa Khrisimasi, ndipo pamene ndikutseka tsopano: "Yesu Khristu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Ndi Mwanawankhosa yemweyo. Iye ali basi Mwanawankhosa lero monga momwe Iye analiri nthawi imeneyo. Iye ali panobe basi monga Iye analiri kumeneko, chifukwa Mawu Ake ndi omwewo. "Kulikonse kumene awiri kapena atatu adzasonkhana mu Dzina Langa, kumeneko Ine ndidzakhala pakati pawo." Ndizo ndendende chimene Iye ananena. Iye samasintha nkomwe, Iye ndi Mulungu Mawu. Iye samasintha nkomwe; akuzipatsabe nkhosa Zake, ndi kuzidyetsa izo pogwiritsa ntchito M'busa Wake Mneneri, chakudya cha nkhosa Zake poyamba. Osati kwa wa fioloje; kwa nkhosa Zake.

206 Iwo sadzatero. . . Kodi ena aja angadye bwanji Iwo. Koma anzeru. . . Zindikirani ichi! Koma anzeru ndi aluntha, ophunzitsidwa bwino padziko, amafunabe kunena kuti kuli Santa Claus. Ndipo kuli zopeka za mitundu yonse ndi zinthu

zimene iwo amazipembedza, chifukwa iwo sangamulandire Iye, Mawu; chifukwa mu zipembedzo zawozo, Iwo sakwanirana ndi zofuna zawo, abusa aganyu amakono a tsikuli. Aganyu ochokera ku kachikhulupiriro, amene angafune kukulumikizitsani inu pansi pa mbuzi imodzi, inu musakhulupirire zimenezo! Iwo adzakutsogolerani inu kumalo ophera nyama. Mvereni M'busa Wamkulu amene anabadwa zaka naintini handiredi zapitazo, mwezi uno. Nthawizina kutaliko, mu Uthenga Wake, kunadza abusa owona amene ankadziwa kusamalira nkhosa.

207 Ndikuzindikira, iwo akufunabe izo. Iwo sangawuvomereze Iwo lero, chimodzimodzi basi monga iwo sanachitire nthawi imeneyo, chifukwa izo sizigwirizana ndi kumverera kwa mpingo wawo. Iwo amawatembenuza Mawu amenewo ndi kuwapanga iwo kuti agwirizane ndi bungwe lawo, ndipo iwo sangalalikire Mawu. Iwo sangatero! Iwo amati, "Chabwino, zimenezo zinali za masiku a atumwi. Izo sizitanthauza *ichi*." Izo zimatanthauza ndendende basi chimene Iwo akunena, Iwo samasowa aliyense kuti. . .?. . .kuwatanthauzira Iwo kwa iwo.

208 Tsopano tiyeni pa ora lino tiweramitse mitu yathu ndi mitima yathu kufumbi la mnthaka, ndipo tifulumire msanga kwenikweni waku khola, kuti tikawone ndi kukalandira Kuwala kumene Mawu awa akuwabweretsa kudzera mwa M'busa: Mneneri-M'busa Wamkulu, Yesu Khristu Mwana wa Mulungu. Ine ndayankhula nanu motalika. Mwinamwake sindinawakonze mawu anga monga momwe atsogoleri achipembedzo akanachitira, ine sindiyesera kuchita zimenezo. Ine ndimayesetsa kuwayankhula Iwo monga momwe Iye akuwaperekera Iwo kwa ine.

209 Koma, kodi inu mukuona chifukwa chimene ankayenera kukhala abusa? Enawo anali ophunzitsidwa kwambiri mu lingaliro linalo mpaka iwo sakanawalandira Iwo. Ndipo lero tiri nawo oyang'anira a mitundu yonse, amzigawo, mabishopu, ansembe, makadinolo, mapapa, chirichonse mdziko, kuyesetsa kuti azititsogolera ife. Koma Mulungu anatipatsa ife M'busa, ndipo M'busa ameneyo ndi Mzimu Woyera.

210 Ndimvereni ine tsopano. "Pamene Iye. . ." (osati lingaliro, *Iye* ndi dzina laumwini) "Pamene Iye Mzimu Woyera adzadza (Mzimu wa Choonadi), Iye adzaulula zinthu izi kwa inu zimene Ine ndazinena kwa inu, ndipo adzakuwonetsani inu zinthu zimene ziri nkudza." Ameneyo ndi M'busa Wamkulu, Ameneyo ndi M'busa amene Yesu anamusiya. Ndipo Mzimu Woyera unalemba Baibulo, Baibulo linanena choncho, "Amuna akale, posunthidwa ndi Mzimu Woyera, ankalemba Mawu." Tsopano, kodi Mzimu Woyera ungakukokereni inu ku kachikhulupiriro? Kodi Iwo ungakukoke—ungakukokereni ku chinthu chimene Mawu awa sakunena? Bwanji, izo zingakhale zosatheka kwathunthu. Mzimu Woyera ungakhale wabodza ngati Iye atanena kuti "*Ichi* ndi chimene mukuyenera kuchita," ndipo

kenako nkutembenuka ndikuti, "Ayi, Iwo unalakwitsa, ndipo inu muzichita zimene mpingo umanena kuti muzichita."

211 Tsopano, ngati mwakhala mukumvetsera kwa chinachake, china chakukokerani inu kutali ndi chenicheni, M'busa woona amene adzakutsogolereni inu ku Mawu, Mzimu Woyera, ndipo inu mulibe chokuchitikirani, ndipo mulibe umboni wa Mzimu Woyera mmoyo wanu, umene popanda. . .

212 Mulungu ndi Mmodzi. Mulungu ndi yekhayo amene ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Iye ndi Moyo Wamuyaya. Ndipo chirichonse chimene chinali ndi chiyambi chiri nawo mapeto. Ndipo ngati mwangokhala membala wa mpingo, iwo unali ndi chiyambi. Koma Mawu a Mulungu alibe chiyambi, Mulungu alibe. . .Ndipo pamene iwe ubadwa mwa Mulungu, iwe umabadwa mwa Mawu, zikatero umadzakhala mwana wa Mulungu, ndipo dzina lako linayikidwa pa Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Ndipo iwe, mtundu wa tsitsi umene uli nawo, mtundu wa maso amene uli nawo, msinkhu umene iwe ulimo, Mulungu anakuwona iwe maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Ndipo Iye anakuwona iwe, munthu, monga momwe iwe uliri. Ndipo ngakhale patabwera zaka millioni komabe, palibe chimene chingakulepheretse iwe kuti ubwerere ku chithunzi changwirocho chimene Mulungu anakusankhira iwe pachiyambi, "Nkhosa zanga zimamva Liwu Langa, mlendo izo sizidzamutsatira."

213 Ndipo ngati simunalandire Moyo Wamuyaya umenewo, usikuuno, ndipo inu mukuyang'ana pa a—a—nkhani yopeka ya mwana atagona mu—a—modyera ng'ombe, ndi gulu la amuna anzeru pamenepo, musakhulupirire zinthu ngati zimenezo. Ndi kuyesera kumaganiza, "Chabwino, ndikhala wabwino. Ndipo ndidzachita *ichi*. Ndipo ndidzajowina mpingo. Ndipo ndizo zonse zimene ndikuyenera kuchita." Inu mwatayika. Ngati mulibe Moyo Wamuyaya, inu mungakakhale bwanji moyo kwa nthawizonse?

214 Inu mukhoza kutenga mbewu ya chimanga, ine sindikusamala momwe ikuwonekera yangwiro, inu mukhoza kuyi-. . .Sayansi inapangapo imodzi, yomwe mukhoza kuyitsegula: ili ndi chinyezi chomwecho, mtundu womwewo wa mtima, zinthu zomwezo zimene mbewu imene imalimidwa kumunda ili nayo, chinthu chomwecho. Inu mukhoza kuziyika izo mu labotale, ndipo simungathe kuzisiyanitsa: yinayo ingapange buledi wa chimanga mwabwino kwambiri monga yinayo, yina ingapange mtundu womwewo wa makonifulekisi. Koma njira yokhayo imene mungadziwire izo, ndi kuzikwirira izo. Imodzi imene munthu anapanga, imakhala pamenepo, imavunda ndipo simatulukanso. Koma imene Mulungu anayipanga, imakhala ndi nyongolosi ya moyo, iyo imakhalanso moyo.

215 Mukhoza kumutsanzira Mkhristu, mukhoza kupita ku tchalitchi ngati Mkhristu, inu mukhoza kulemba dzina lanu pa bukhu ngati Mkhristu, inu mukhoza kujowina chipembedzo ngati Mkhristu; zimenezo zikhoza kukhala zabwino, koma pokhapokha ngati Moyo Wamuyaya umenewo uli mwa inu chimene M'busa Wabwino ameneyo anaperekera Moyo Wake, kuti adzadzigawanize. . .Pamene Mulungu anatsika pa Pentekoste, Iye anatsika mu mpira wamoto monga Iye anachitira pa Phiri la Sinai, monga Iye anachitira kwa m'busa woyamba, Mose. Ndipo pamene Iye anabwera pansi, Iye anadzadzigawaniza Iyemwini mmalirime a moto amene anakhala pa aliyense wa iwo, Mulungu kudzigawaniza Iyemwini mwa anthu Ake. Ndipo pokhapokha mutalandira icho chimene. . .Petro ananena kuti "Ndi cha kwa inu, ndi kwa ana anu, kwa iwo akutali."

216 Amzanga, musamvere nthano iliyonse ya fioloje, inu mubadwe kachiwiri. Ndipo pamene inu mutero, Mzimu umene uli mwa inu ndi gawo la Mulungu, ndipo umachitira umboni ku Mawu aliwonse a Mulungu kukhala "Choonadi." Ngati inu mulibe chokuchitikirani chimenecho, tiyeni tsopano tifulumire kupita modyera ng'ombe, Mawu. Tiyeni tithamangire ku Baibulo, titalikirane ndi matchalitchi okongoletsedwa otchulidwa ndi fioloje awa, tipite modyera ng'ombe mwenimwenimo, ku Mawu a Mulungu kumene Mesiya amadziwitsidwako.

Ndi mitu yathu yoweramitsidwa, tiyeni tipemphere.

217 Wokondedwa Mulungu, ndizo zonse zimene ine ndikudziwa kunena pa nthawi ino. Ife tikuyandikira Khrisimasi, misewu yadzadza ndi amuna ndi akazi, anyamata ndi atsikana, akukankha, akududa, akuyesetsa kuti agule mphatso kuti akapereke kwa winawake amene angawapatsenso chimodzimodzi. Anthu ambiri amene amadzitcha okha Akhristu ali kunja mmisewu akugula ndudu, mowa, ngati mphatso za Khrisimasi. Mulungu, zikuwoneka ngati iwo akuponyera izo mobwezera pa nkhope Yanu, kumaphunzitsa ana awo zopeka zina, Zachiroma, fioloje yachikunja ya Nikolasi Woyera, nthano ina imene imavomerezedwa mophweka ndi dziko, ndipo amakana Khristu weniweni wa Khrisimasi, Mwanawankhosa weniweni.

218 Mulungu, ine ndikupemphera, usikuuno, kuti pamene tiri ndi mitu yathu yotembenuzidwira kufumbi kumene Inu munatitengako,. . .Inu munamuuza Abrahamu kamodzi, mneneri-m'busa wamkulu, "Tuluka, Abrahamu, ndipo ukawerenge mchenga umene uli mmbali mwa nyanja."

219 Ndipo iye anayankha, "Iwo ndi wosawerengeka, ine sindingathe kuwuwerenga."

220 Kenako Inu munati, "Yang'ana mmwamba, ndipo uwerenge nyenyezi." Ndipo iye anadziwa kuti izo zinali zosatheka. Ndipo Inu munati kwa iye, "Chomwechonso mbewu yako idzakhala." Ife tikuyang'ana pa uthenga uja kwa m'busa-mneneri, "kuchokera ku fumbi lapansi, mpaka nyenyezi za kumwamba," kuti ngakhale pangakhale imfa m'matupi athu achivundi ikutitengera ife kufumbi, pali Moyo umene ungatiwukitse ife kupita ku nyenyezi.

221 Monga Inu munanena kwa mneneri Wanu wamkulu Daniele, "Ndipo iwo amene adzamdziwa Mulungu wawo, mmasiku otsiriza, adzachita zazikulu. Ndipo iwo amene adzatembenuzira ambiri ku chirungamo adzawala kuposa nyenyezi kwa nthawi za nthawi."

222 Ambuye Mulungu, Mlengi Wamkulu, Amene anali wofunitsitsa kwambiri kubwera pa dziko lapansi mmawonekedwe a Yesu, kuti munthu adzadziwe chimene Mulungu anali. Ndipo Inu munali Mmodzi yekhayo amene mukanakhoza kutenga chilango cha imfa, panalibe Mngelo, panalibe mlowammalo amene akanachita zimenezo. Inu munali Mmodzi amene munapereka chilangocho, ndipo Inu nokha mukanachichotsa molungama icho. Ndipo pokhala Mzimu, Inu simukanakhoza kufa. Koma Inu munasandulika thupi kuti Inu mudzakhoze kufa; ndi kudzakhala Mwanawankhosa kuti Inu mudzachotse tchimo la Owomboledwa Anu, amene Inu munayenera kuwawombola iwo ndi Magazi Anu Omwe.

223 Oh, nkhaniyo ndi yopambana kwambiri, Ambuye, imadutsa pa mitu ya ambiri. Kuganiza: "Yehova Wamng'ono, atagona modyera, Iye ankayenera kukhala ngati mwana. Yehova wamng'ono, wobadwira mu khola. Yehova wamng'ono, akusewera ndi ana mu msewu. Yehova wamng'ono, wausinkhu wa zaka za m'matini. Yehova wamng'ono, mwana wasukulu. Ndipo Yehova, Wamphamvuyo." Inu munatenga malo onsewa. "Ndipo kenako, Yehova, Mwanawankhosa. Yehova, Mneneri." Ndipo Inu munadzakhala zonse izi kuti Inu mudzakhoze kuvutika ndi chilango cha tchimo, ndi kudzatipatsa ife Moyo Wamuyaya.

224 Tikhululukireni ife, O Mulungu, ife, zolengedwa zosauka, zosayenera za dziko lino. Ife tachititsidwa manyazi usikuuno, Ambuye, pamene ife tiwerenga zimene Inu mwatichitira ife, ndipo zapang'ono kwambiri zimene ife tachita pobwezera. Momwe Inu munabwerera mmasiku a atsogoleri achipembedzo aakulu! Momwe Inu munali wololera kuyima ndi kunyezimiritsa Mawu a Atate! Momwe Inu simunanyengerere pa malingaliro awo! Ndipo lero zikuwoneka ngati palibe amene akufuna kuimirirapo ndi kuwatcha Mawu akhalebe "Mawu," ndipo osanyengerera. Ife tikupemphera, Mulungu, Inu mutikhululukire ife pa zinthu izi zimene ife tazinyalanyaza kwambiri. Ndipo mutipatse ife usikuuno, mmitima mwathu,

pamene ife tikupereka kwa Inu ngati modyera. Ndipo ife tikudziwa kuti nthawi iliyonse imene Khristu Wopachikidwayo walandiridwa, pamakhala kubadwa mwatsopano, pamakhala nkhosa yobadwa kumene, kumakhala kuyimba Kumwamba ndi Angelo. Pa wochimwa mmodzi amene walapa, Angelo amayimbanso.

225 Ife tikupemphera, Mulungu, kuti ngati pangakhale ena usikuuno amene sakukudziwani Inu ngati Mphatso yeniyeni ya Mulungu, ngati Mpulumutsi wawowawo, osati kungokhala mwa kuganiza kwa mmalingaliro, koma mwa kubadwa mwatsopano (pobadwa mwa Mzimu Wanu), mulole iwo awulandire Iwo pakali pano, Ambuye, ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Ndipo ngati pangakhale mmodzi, Ambuye, amene sanachite izi, mulole mitima yawo ilandire chimwemwe tsopano, ndipo akampeze monga abusa akale, modyera mwa mtima wawo, Mawu, Mesiya; amene atsimikiziridwe kwa iwo ngati Mzimu Woyera, M'busa Wamkulu wa tsikuli. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu.

226 Pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ndipo ine ndikudalira mitima yathu yaweramitsidwa, inu munga—inu mungatero, m'bale wanga wokondedwa, ngakhale iwe utakhala membala wa tchalitchi. . . Ndipo ine ndikuyembekeza kuti sindinakupwetekeni inu ponena zimene ndanenazi. Ine. . . Ndi chabwino kukhala wa tchalitchi, ife tiyenera kuchita zimenezo, koma, O m'bale, basi musangovomereza izo, mukuyenera kubadwa kachiwiri. Icho ndi chimene Mneneri-M'busa Wamkulu ananena, "Mukuyenera kubadwa mwatsopano." Iye ananena izo kwa wa fioloje, "Mukuyenera kubadwa mwatsopano."

227 Ndipo mukabadwa mwatsopano, sizimangokhala chifukwa chakuti mumakhulupirira. Iwo amati, "Iwe umabadwa pamene iwe wakhulupirira."

228 Koma Baibulo linati, "Mdierekezi amakhulupirira, nayenso." Tsopano, zindikirani, sizimenezo ayi, ndi chokuchitikira.

229 Inu mukuti, "Chabwino, ine ndakhala moyo wabwino."

230 Chomwechonso atumwi ankachita, koma iwo anali asanabadwe kachiwiri kufikira atalandira Mzimu Woyera. Iwo anali asanatembenuke nkomwe mpaka iwo atalandira Mzimu Woyera. Inu mukukumbukira usiku asanamupereke. . . kapena pamene anamupereka, kumupereka kusanachitike? Yesu anati kwa Simoni Petro, "Iwe ukadzatembenuka, ndiye udzawalimbikitse abale ako." Ndipo Petro anamutsata Iye zaka zitatu ndi theka, ndipo ankatulutsa ziwanda, ndi kuchiritsa odwala, anali atalalikira Uthenga, ndipo komabe (molingana ndi Mawu) anali asanatembenuke nkomwe.

231 Tsopano, kodi mungafune mtundu umenewo wa—wa Mtumiki mu mtima mwanu usikuuno? Ngati—ngati mukufuna

Iwo kwenikweni. . .Sizimapanga kusiyana kulikonse chimene winawake anganene, Iwo ndi owona, m'bale, mlongo. Ine ndikudziwa kuti zimenezo ndi zoona. Kodi mungatero, pamene mutu uliwonse waweramitsidwa ndipo diso lirilonse latsekedwa, osati kwa ine, ndine munthu chabe, m'bale wanu, koma kwa Khristu mungakweze dzanja lanu, ndikuti, "Ndikukhulupirira Iwo. Ndipo ndikumufunadi Khristu ameneyo mu mtima mwanga, Khristu weniweni wa Khrisimasi"? Kodi mungakweze dzanja lanu tsopano? Mulungu akudalitseni. Izo nzabwino. Mulungu akudalitseni inu, nanunso. Mulungu akudalitseni inu. Mai, manja paliponse.

232 Mulole izo zichitike, m'bale; mulole izo zichitike, mlongo; mulole izo zichitike, mzanga; mudzadzidwe ndi Mzimu wa Mulungu. Kodi zimapanga kusiyana kotani chimene wina aliyense amanena? Kumbukirani, ndi moyo wanu. Ife tikhoza kusadzakhala pa dziko lapansi mmawa, ife tiribe—tiribe chitsimikizo cha moyo wina woposa umene ife tikuwupuma m'mphuno zathu tsopano. Ife mwina tikhoza kusapanganso kupuma kwina, kokha chisomo cha Mulungu. Ndipo icho nchaubwino wanji, ziribe kanthu momwe wakhalira wabwino ndi chimene. . .? Yesu anati, "Pokhapokha ngati munthu abadwa kachiwiri, iye mwanjira iliyonse sadzalowamo."

233 Tsopano, ndikudziwa *matchulidwe* a chimene kubadwa kachiwiri kuli, koma tiyeni tingowona chimene chinachitika mu Baibulo pamene iwo anabadwa kachiwiri. Petro anali wokhulupirira, atumwi anali okhulupirira, koma iwo anali asanabadwe mwatsopano mpaka Mzimu Woyera utawagwera iwo pa Pentekoste. Tsopano, ankadabwa chimene chinachitika, ndipo Petro anati, ndi ena onsewo, "Inu amuna a Israeli, ichi chidziwike kwa inu; Yesu waku Nazareti, munthu wovomerezeka ndi Mulungu mwa inu mwa zizindikiro ndi zozizwitsa ndi zodabwitsa, zimene Mulungu anachita mwa Iye; Iye amene anadziwidwiratu, ndi gulu lokhazikika inu munamutenga ndi manja oyipa ndi kumupachika, Amene Mulungu wamuukitsa ndipo ife ndife mboni Zake. Iye wachita izi zimene inu mukuona ndi kumva tsopano, ndipo ndi mogwirizana ndi Malemba."

234 Ndiyeno, pamene iwo anamva izi, analaswa mu mtima mwawo, ndipo anati, "Amuna ndi abale, tingatani kuti tipulumutsidwe?"

235 Petro anati kwa iwo, "Lapani!"

236 Tsopano, mzanga Wakatolika wakhala apa, amene ine ndikudziwa za anayi kapena asanu a inu mwakhala pano. Ine ndimakambirana izi ndi wansembe wanu, mwinamwake osati wansembe *wanu*, koma mmodzi wa ansembe Akatolika, iye anati, "Yesu anawupatsa mpingo mphamvu yokhululukira machimo, 'Aliyense amene iwe umukhululukira, kwa iwo akhululukidwa; aliyense amene mudzasunga machimo ake, kwa

iwowo asungidwa.'" Izo nzoona. Koma tiyeni tiwone momwe iye anachitira izo, momwe atumwi anatsatirira kutuma Kwake, osati molingana ndi momwe—momwe wansembe amachitira lero.

237 Koma kodi wansembe woyamba anachita chiyani, ngati inu mukufuna kumutcha iye chomwecho, Petro, amene anali ndi mafungulo aku Ufumu, iye ananena kuti tizichita motani izo? Iye anati, "Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo, ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana." Ndipo ngati Mulungu akuyitanabe, chochitika chomwecho chiri kwa inu ngati mungatsatire mankhwala omwewo. Ngati osonkhana ano amakhulupirira Zimenezo, ndi mitu yanu yoweramitsidwa, nenani, "Ameni." [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Ndiye, chirichonse choperewera pa Zimenezo ndi chosiyana ndi Mawu, ndipo si molingana ndi M'busa.

238 Ambuye Yesu, iwo ali mmanja Mwanu tsopano. Ndikupemphera kuti mtima uliwonse wotseguka usikuuno umene ulibe Khristu, Mesiya (ndipo Khristu ndi Mawu, Mawu odzodzedwa akuwonetseredwa), ndipo ngati pali mitima yotseguka usikuuno imene ilibe Mesiya, Mphatso yeniyeni ya Khrisimasi, Mphatso yeniyeni ya Khrisimasi imene ilipo, imene Mulungu anapereka kudziko lapansi, ndi kuilengeza Iyo ku dziko lapansi kudzera mwa abusa, a Mwanawankhosa Wake, Chitetezero cha tchimo, ndipo ngati mtima umenewo watseguka usikuuno, ikani mmenemo, Ambuye, Mawu a Mesiya a lero. Ife tikuwapereka iwo kwa Inu mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana Wanu. Ameni.

239 Kodi inu mumamkonda Iye? Kodi inu mumamkhulupirira Iye? "Funani inu poyamba Ufumu wa Mulungu, ndi chirungamo Chake, zinthu zina zonsezi zidzawonjezeredwa kwa inu."

240 Amzanga, tisanabalalike, ndikufuna kuti ndinene ichi. Nthawi zambiri, sindimamvetsetsedwa kwambiri. Ndiri ndi Uthenga wochokera kwa Mulungu, ndipo ndikuyenera kulengeza Uthenga umenewo posatengera chirichonse. Ine ndikudziwa kuti Iwo sumamvetsetsedwa. Ngati Iwo ukanati usamatero, ndiye Iwo sukanakhala Uthenga wa Mulungu; Iwo sukanakhoza kukhala. Pali zovuta zambiri masiku ano kuti Iwo usamvetsetsedwe. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu ali ndi anthu mu chipembedzo chirichonse ndi bungwe la mdziko, ndipo sikuti ine ndikutsutsana ndi abale anga. Ine ndinabwera kuno ku Tucson, zaka zitatu zapitazo, ndipo ndinali ndi msonkhano ndi inu atumiki uko kwa M'bale Gilmore, ndipo panafunsidwa, kodi ine "ndinabwera kuno kudzayambitsa mpingo?"

241 Ine ndinati, "Ayi, bwana. Ndabwera kuno kudzakuthandizirani *inu*." Koma ine sindinafunsidwebe, mzaka zitatu. Komabe chimodzimodzi, ine ndiri kuno kuti ndidzakuthandizireni inu. Ine ndiri kuno kuti ndidzagwirane manja ndi inu, osati kudzajowina mabungwe ndi inu, koma kudzagwirana manja ndi mtima ndi inu pa Mawu a Mulungu, kudzayesetsa kulalikira Uthenga kwa moyo uliwonse wotayika ndi munthu aliyense wosowa amene alipo pansi pakuwomba kwa maliwu athu.

242 Ine ndikudzipereka ndekha kwa Mulungu, usikuuno, ndi mtima wanga wonse, ndi zonse zimene ziri mwa ine. Ndiribe zochuluka zoti ndizipereke; ine sindingabweretse lubani, mure, ndi golide, chifukwa ine ndiribe. Koma zonse zimene ndiri nazo mwa inemwini zimene Mulungu anandipatsa ine, moyo uno, ine ndikuzipereka izo kwa Iye mwatsopano usikuuno, pa chodyera cha Mawu Ake mu mtima mwanga; ndipo ndikumulonjeza Iye, kuti ndiima ndi Mawu amenewo, ngati Iye ati andilole ine kuti ndikhale moyo chaka china, mokhulupirika basi momwe ine ndingaimire; kulalikira chidutswa chirichonse cha Iwo, ndi kukhulupirira chidutswa chirichonse cha Iwo; chotero, ndithandizeni ine, Mulungu. Kodi inunso muchita chimodzimodzi ndi ine?

243 Tilandireni ife, Ambuye. Ife tikulandira Mphatso Yanu ya Khrisimasi, Mesiya, Mawu odzozedwa amene akutsimikizira Kukhalapo Kwanu ndi ife, Ambuye, mosalabadira kachikhulupiriro kapena chipembedzo. Ife tikudzipeza, tokha lero, dziko likupasuka, ndipo apa Mesiya wamkulu wayimirira atatambasula manja Ake: Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, amene anapanga malonjezowo, kuti mu masiku otsiriza ano, mpingo udzakhala bungwe kwambiri mpaka iwo udzapita kukalowa mu Laodikaya. Ndipo ife tikuziwona izo lero, Ambuye.

244 Kodi tingachite chiyani, wokondedwa Mulungu? Ine ndingachite chiyani? Ndithandizeni ine ndi azibusa ena awa, Ambuye, kuzungulira dziko, azibusa a Mawu, kuti tikalengeze Iwo, Ambuye, mu chaka chikubwerachi. Tithandizeni ife, Ambuye, ife tikupemphera. Tipatseni ife za Chikondi Chanu ndi Mzimu Wanu ndi Kuwala Kwanu. Tikudzipereka tokha usikuuno ku Mawu Anu ndi ku kuyitana Kwanu. Mu Dzina la Yesu Khristu, tikulandira Mphatso Yanu ya Khrisimasi: Mawu a Mulungu akusandulika thupi mwa ife. Ameni.

245 Ine ndimakonda nyimbo za mpingo. Paulo anati, mu Baibulo, "Pamene ine ndinaimba, ine ndinaimba mu Mzimu. Ndimalalikira, ndimalalikira mu Mzimu. Pamene ine. . . chirichonse chimene ine ndichita, ine ndimachita icho chonse mu Dzina la Yesu Khristu." Tsopano, pokhala kuti Izi zakhala zovuta pa inu. . .Ndipo ine—ine ndimakuyamikirani inu. Ine ndikubwera ndi Uthenga uwu. Nthawizina zimawoneka ngati

ine ndimangodana nazo kuti ndinene Izo, komabe ndine—ndine wokakamizidwa, abale. Ngati sindichita zimenezo, ndine wachinyengo. Ngati sindichita zimenezo, ndine wompereka ku chikumbumtima changa chomwe, ndiponso changa chomwe—chikhulupiriro changa mu Mawu a Mulungu. Ndikuyenera kuchita zimenezo, osati kuti ndikhale wotsutsa, koma kuti ndikhale woona ku mayitanidwe anga. Ndipo ine ndikufuna kuti ndikuthandizeni inu nonse, ndikufuna kuchita chirichonse chimene ndingathe.

246 Tsopano tiyeni tiyimbe imodzi mwa nyimbo zopambana ya nthawi zonse, ndimaikonda iyo kwambiri, *Ine Ndinkonda Iye*. Inu mukudziwa, ndikukhulupirira ngati ife tonse tikanamamukonda Iye, bwenzi tikuchita chimene Iye anatiuza ife kuti tizichita. "Mukunditcha bwanji Ine, 'Ambuye,' ndipo osamachita zinthu zimene Ine ndakulamulani kuti muchite? Mumanditcha bwanji Ine, 'Ambuye,' ndipo kenako osachita chimene Ine ndinakuuzani kuti muchite?"

247 Kodi mungakonde kumvera m'busa waganyu amene angati "lembani dzina lanu pa bukhu, ndipo mujowine; tengani mgonero uwu, nenani *ichi*, ndipo zonse ziri bwino," pamene M'busa Wamkulu Mwiniwake anati "pokhapokha munthu atabadwa kachiwiri sangathe kuwuwona Ufumu wa Kumwamba"?

248 Ndipo yang'anani pa a fioloje ophunzitsidwa awo a tsiku limenelo, ophunzitsidwa! Woyera? Kukhala moyo woyera? Palibe chimene tingafanizitse nacho lero, momwe iwo ankakhalira. Ndipo kodi M'busa Wamkulu anawatcha iwo chiyani? Anati, "Inu ndi a atate wanu mdierekezi," chifukwa iwo sanatero... Iwo anawazindikira Mawu, koma Mawu a tsiku lina, osati Mawu a tsiku *limenelo*.

249 Ngati iwo anazindikira nthawi ya Nowa, izo zonse nzabwino, imeneyo inali nthawi ya Nowa; koma izo sizikanagwira ntchito mu nthawi ya Mose. Ndipo nthawi ya Mose siikanagwira ntchito mu nthawi ya Khristu. Mukuona? Nthawi ya Luther siingagwire ntchito mu nthawi ya Wesley. Nthawi ya Wesley siingagwire ntchito mu nthawi ya Pentekoste. Ndipo Pentekoste yachita chinthu chomwe chomwecho chimene ena onsewo anachita. Tsopano, ndani wandithandiza ine mmasiku apitawo? Ndakufunsani inu.

250 Pamene tsamba la udzu litulukira, ndi chiyani chimenecho? Chiyani...pamene tsamba la tirigu litulukira. Yesu anati, "Pokhapokha ngati njere ya tirigu igwera mu nthaka." Chimachitika ndi chiyani pamene mbewu ya tirigu...kapena tirigu akagwera mu nthaka? Chinthu choyamba chimene chimatuluka ndi tsamba laling'ono. Ndi—si monga tirigu amene analowa pansi. Taonani chirengedwe. Sizimakhala monga njere

yomwe inalowamo, koma ndi chonyamulira Moyo wa njere. Chimene chinabwera . . .

251 Wosakhulupirira uja amene analemba bukhu lotchuka, *Mulungu Wa Chete*, ilo linati, "Zingatheke bwanji kukhala Mulungu amene angatsegule Nyanja Yofiira, ndi kuyima kudutsa zaka sauzande za mibadwo yamdima ndi kuwawona ana aang'ono akudyedwa ndi mikango, ndi anthu atapachikidwa pa mitanda, ndi kumaphedwa mmabwalo ndi zinthu, ndipo sanatsegule konse pakamwa Pake?" Mwaona, Mawu ndi vumbulutso.

252 Tirigu ameneyo, pamene tirigu weniweni uja anayamba pachiyambi, iye anamukhumudwitsa Mulungu. Ndipo potsiriza panadzabwera Tirigu, chonyezimiritsa chenicheni cha Mulungu, chimene chinadzanyezimiritsa Mawu Ake onse mpaka kuti Iye anadzakhala Mawu. Kenako Mulungu anamupatsa Iye Mkwatibwi pa Pentekoste; koma Mkwatibwi ameneyo anagwera mu nthaka kudutsa mu mibadwo ya mdima, chimodzimodzi monga momwe tirigu weniweni anachitira, Iye anagwera mkati. Ndipo ndi chifukwa chiyani iye sanataketake? Chifukwa iye anali atabisidwa pansi mnthaka, iye ankayenera kuti avunde asanabweretse moyo.

253 Koma pamenepo panadzabwera wansembe wamng'ono nthawi ina, dzina lake Martin Luther, ndipo iye anatulutsa Mawu amodzi a Choonadi: "Olungama adzakhala moyo mwa chikhulupiriro," pamenepo panadzabwera tsamba; kenako tsamba lina linatsatira, Zwingli, ndipo kenako panadzabwera Calvin ndi Knox mpaka pansi.

254 Chinthu choyamba inu mukudziwa, iye anasintha tsamba lake, iye analowa mu ngayaye. Tsopano, zimenezo zinkawoneka pang'ono pokha monga iye, komabe sizinali kwenikweni chinthu chimene chinapita pansi, apo panadza Wesley motsatira. Kuchokera mwa Wesley panadzabwera mpingo wa Methodisti, kuchokera ku mpingo wa Methodisti kunadzabwera a Nazarene, United Brethren, ena otero. Iyo inachita chiyani? Iyo inagweranso mmbuyo ndipo inabereka, zinkawoneka ngati njere yeniyeni ya tirigu tsopano, Pentekoste.

255 Tsopano, tamuwonani Yesu, mu Mateyu 24:24, "Mu tsiku lotsiriza, mizimu iwiri idzakhala yofanana kwambiri mpaka iyo ikanadzanyenga Osankhidwa omwe, ngati kukanakhala kotheka." Tsopano, pamene njere ya tirigu imeneyo inadzatulukira, wolima tirigu aliyense amadziwa kuti iye amawoneka ngati njere yangwiro, ya tirigu. Koma inu mukhale pansi ndipo muigwire iyo mdzanja lanu, muitsegule iyo. Mulibemo tirigu mkati mwake, ndi mankhusu. Koma mmbuyo kumbuyo kwenikweni, pansi pa galasi lowunikira mukhoza kuwona mphukira yaying'ono, pamenepo pakubwera njereyo. Ndipo kenako mankhusu amenewo ndi oti achite chiyani?

Ndi oti ayiteteze njereyo, dzuwa lotentha likhoza kuyipha iyo, iwo amayiteteza njereyo kufikira njereyo itakhwima. Ndipo kenako njereyo ikakhwima, mankhusuwo amachoka kwa iyo. Koma, kodi inu munazindikira, njere imeneyo ndiye imene inabwerapoyo, imayenera kukhala mtundu womwewo wa njere imene inalowa mu nthaka.

256 Chitatha chitsitsimutso cha Luther, kunadzabwera bungwe. Chitatha chitsitsimutso cha Wesley, kunadzabwera bungwe. Atachoka Alexander Smith, John. . . Alexander Campbell, John Smith, onse a iwo, kunadzabwera bungwe. Itatha Pentekoste, kutsika pansi monga chinthu chenicheni, koma kunadzabwera bungwe. Ilo linachita chiyani? Linadzichotsapo.

257 Ife takhalapo nazo zaka fifitini za chitsitsimutso, sichinachidziwikepo konse mu mbiriyakale yonse. Ndipo penyani, mu zaka fifitini izi za chitsitsimutso, Icho chasesa kuzungulira dziko, ndipo palibe bungwe limodzi limene lamangidwa kuchokera mwa Icho. Icho chinali kuti? (Icho chinayambitsa mvula yamasika, icho chinafa mu chake. . . pomwepo, icho chinafa.) Sipanakhaleko bungwe lotsatira Ichi. Bwanji? Ndi njere Yokha, sipangakhalenso zina. Ndipo mankhusu tsopano akukungunukapo, palibe mgwirizano, palibe amene akukufunani inu. Chifukwa chiyani? Icho chikuyenera kukhala Chimenecho.

258 Nchifukwa chiyani mpingo umenewo unayikidwa pamenepo? Kuti udzathandizire Icho. Kumene. . . Ndani adzagwirizane nacho? Ndi Baptisti uti, kapena Wachipresbateria, kapena Wachilutera amene akanathandizira kampeni ya machiritso Auzimu? Tsopano pamene Choonadi chibwera, chimachitika ndi chiyani? Osati mankhusu; koma Moyo umatuluka kuchoka mu mankhusu, kupita mpaka mu njere, Moyo weniweni woona. Bungwe limayima pamenepo, limafa, monga momwe limachitira mu m’badwo uliwonse, likuchitanso chimodzimodzi. Inu munatuluka mu zimenezo, zaka fifite zapitazo, ndipo mwabwereranso mmenemo kachiwiri! Koma Moyo weniweni umatsatira njere, ife tiri pa nthawi yotsiriza, abale.

259 Kodi iwo anachokeranji? Kuti zikabweretse njereyo pamaso pa Mwana, kuti akakhwimitse njereyo ku kukhwima kwa golide kwa Mbuye. Nchifukwa chiyani iwo achokapo? Kuchitira kuti, zikayambitse kupweteka kwa mtima, misonzi, kuti sakukhala pamaso pa d-z-u-w-a, koma M-w-a-n-a, kuti ikakhwimitsidwe ku Uthenga wathunthu woona, kuti akawonetsere chirichonse chimene Yesu Khristu analonjeza mu Baibulo. Pakuwuka Thupi lero pakati pa anthu. Ndipo sipadzakhalanso mabungwe, iwo akupita mpaka ku Laodikaya wolemera. Kodi bungwe lachita bwino ndi chiyani? Mamillioni a madola, ndi mamillioni a miyoyo.

260 Ndipo kodi M'busayo anachokera kuti? Kuti adzawawombole abale Ake ku msinga. Ine—sindikudziwa; Mulungu, mukhale nafe, tithandizeni ife. Kawerengeni Mawu! Fufuzani Malemba! Mwa Iwowo ife timaganiza kuti tiri ndi Moyo Wamuyaya, ndipo Iwo ndi Amene amachitira umboni za Choonadi. Mwaona, Mulungu anayika Mawu Ake ku m'badwo uliwonse. M'badwo uno nthawizonse. . .

261 Kodi Yesu ananena chiyani pamene Iye anabwera? Iye anati kwa anthu amenewo, "Onyenga inu! Inu mumayeretsa makoma, ndi kumanga manda a aneneri, ndipo makolo anu anawayika iwo mmenemo. Ndipo inu ndi ana a makolo anu. Ndipo ntchito zimene iwo ankachita, inunso muzichita." Izo zimakhalabe chimodzimodzi, abale anga.

262 Koma pamene Yesu adzabwera tsiku lina, M'busa Wamkulu wa nkhosa kuyambira Pentekoste kudzera mwa Luther kudutsa mibadwo yonse, amene akulandira Kuwala pamene Iko kumabwera kudutsa mwa zonyamulira (osati kuvomereza chonyamulacho, anavomereza Kuwala; mwaona, anatuluka), Iye adzabwera kudzawombola. Ndine wokondwa kuti ndikudziwa kuti Iye akubweranso. Oh, kodi inu mudzawerengedwa ndi gulu Lake? Kodi inu mudzawerengedwa? Pali njira imodzi yokha yochitira izo, osati mwa kujowina mpingo, koma pobadwira mwa Iye. "Ndipo onse amene Atate andipatsa Ine, adzabwera kwa Ine, ndipo palibe munthu angabwere pokhapokha Atate Anga atamuyitana." Mwaona, ndizo zonse zimene ziripo kwa izo, alandireni Iwo. Iye. . .Ndiyo Mphatso ya Khrisimasi yokhayo imene ndimaidziwa, ndi mphatso ya Mulungu imene Iye anayipereka kwa dziko lapansi, Mwana Wake wobadwa yekha yekhayo. Ndipo Iye ali yemweyo, dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Mawu. Mukuona? Mukhulupiririreni Iye mu tsiku lino, chidzalo cha Baibulo.

263 Pamene zinsinsi seveni zimenezo. . .Kubwerera kudutsa Mibadwo Seveni ya Mpingo imeneyo, panali zinsinsi seveni zobisika. Ine ndikulemba bukhu la Izo. Ndipo wa fioloje wamkulu anati kwa ine osati kale kwambiri, anati, "M'bale Branham. . ." Mukuona momwe Satana amayeserera kuti akuchotsepo iwe panjira? Iye anati, "M'bale Branham, inu mukudziwa chiyani? Ine ndikukhulupirira kuti Ambuye awulula kwa inu choti tichite chotsatira. Ndi ku. . . chidzakhala chinsinsi china chachikulu chimene chabisidwa pansi pa Zisindikizo Seveni."

264 Ine ndinati, "Ayi, si choncho, m'bale."

265 Iye anati, "Icho chidzakhala chinachake chimene sichinalembedwe nkomwe ngakhale mu Mawu."

266 Ine ndinati, "Ayi! Ayi! Iwe ukuyiwala, 'Aliyense amene adzawonjezera mawu amodzi, kapena kuchotsa Mawu amodzi.'" Mwaona, Iwo ali kale mmenemo, koma okonzanso analephera

kuwawona Iwo, iwo sanakhale moyo motalika mokwanira kuti awawone Iwo.

267 Ndipo mibadwo inatha tsopano, ife tiri komwe kuno ku Laodikaya. Ndipo kumbukirani, m'badwo wa Laodikaya, Iye anali kunja kwa mpingo, akugogoda, akuyesera kuti abwerere mkati: Eva anali atamutulutsa Adamu wake kunja. Mulungu, tithandizeni ife. Mutilole ife tipite kudutsa msasa kuti tikamupeze Iye. Tiyeni tikazunzike kunja kwa zipata ndi Iye. Tiyeni tipite kwa Iye mu imfa Yake, mu kuyikidwa mmanda Kwake, ndi mu chiwukitsiro Chake; pakuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

268 Tiyeni tiyimbe nyimbo imodzi tisanachoke. Kodi inu mutero? *Ine Ndinkonda Iye*. Kodi mungatipatse poyambira, mlongo? Ndi angati amaidziwa nyimbo yakaleyo? Ine. . .Ngati inu munakhalapo mu misonkhano, ine ndimayikonda iyo.

269 Tsopano tiyeni tingotseka maso athu, taganizani za Yehova. Palibe amene anali woyenera, palibe amene akanatha kuchita izo koma Iye. Ndipo Iye anabwera pamenepo, ndipo anadzakhala mwana wamng'ono. Iye anadzakhala, wachinyamata. Iye anadzakhala kalipentala, munthu wogwira ntchito. Iye anadzakhala Mwanawankhosa, Iye anadzakhala nsembe. Iye anawuka mwachigonjetso, Yehova. Ndipo monga Mose anatulutsa dzanja lake kulichotsa mchifuwa mwake kuchoka pamtima pake, Mulungu anachotsa dzanja Lake mu chifuwa Mwake (chinsinsi Chake) Mwana Wake amene anakanthidwa ndi matenda a tchimo, osachiritsika; ndipo analiyikanso Ilo mchifuwa kachiwiri, ndi kulichotsa Ilo ndi kulitambasulira Ilo kwa inu ndi ine: "Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse."

270 Yang'anani pa Iye tsopano.

> Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
> Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
> Nandigulira chipulumutso changa
> Pa mtengo wa Kalvare.

271 Ndi angati akudziwa kuti ankayenera kukhala m'busa, nenani "Ameni." [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Akuyenera! Chifukwa chiyani m'busa? Zinkayenera kutero. Tsopano pamene ife tikuyimbanso ndime iyi mobwereza, fikirani pa tebulo. Pali Amethodisti, Baptisti, Lutheran, Presbateria, Katolika, ndi onse, akhala muno usikuuno. Gwiranani chanza, ndikuti, "Mwendamnjira mzanga, ndine wokondwa kwambiri kukhala pano ndi iwe, usikuuno." Nenani chinachake kwa iwo. Nenani, "Mulungu akudalitse iwe," pamene tikugwirana chanza wina ndi mzake tsopano. Pamene ife tikuyimba iyo kenanso tsopano.

> Ine. . .[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].
> . . .chipulumutso changa

Pa mtengo wa Kalvare.

272 Tsopano tiyeni titseke maso athu ndipo tikweze manja athu, ndipo timuimbire Iye.

Ndinkondani Iye, ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

273 Ndipo tsopano, Mulungu wopanda mawonekedwe. Chotero, tiyeni tiweramitse mitu yathu ndipo tiying'ung'udze iyo tsopano, monga ana aang'ono, ndinu ana a Mulungu. Musayang'ane pa chimene dziko lingaganize, mukupembedza tsopano, kumupembedza Khristu. Ingoweramitsani mitu yanu ndi kuing'ung'udza iyo. [M'bale Branham akung'ung'uza *ine ndinkonda Iye*—Mkonzi.]

274 Kodi inu simukumverera ngati mwakhulidwa yense? Basi ngati Chinachake changochotsa kukaikira konse ndi chidziko kutali ndi inu? Mukumverera chomwecho? Kwezani mmwamba manja anu, "Ndikungomverera kuti ndakhulidwa. Ine ndikumverera mosiyana. Ine ndikumverera ngati kuti ndakhala ndikudya kuchokera mmanja Mwake. Ine ndi . . ." Monga m'bale pano anachitira umboni, "Chakudya, Chakudya cha M'busa, Chakudya cha nkhosa." Amenewo ndi Mawu.

275 Nkhosa za Mulungu zimadya Chakudya Chake, "Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu aliwonse otuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu." Ndipo ili ndi Amenewo, Baibulo. Ife timadya Mawu aliwonse, osati Mawu ena okha, koma Mawu aliwonse amene atuluka. Oh, kodi izo sizikukupangani inu kumukonda Iye? Kuganiza kuti tsopano tiri ndi Moyo Wamuyaya! Osati tidzakhala nawo, *tsopano* ndife ana a Mulungu. Osati tidzakhala, tsopano! Ndipo takhala pamodzi mmalo am'mwambamwamba *mwa* Khristu Yesu. Ndipo televizioni yaikulu, imene imalengeza kuti pali funde limene limapangitsa anthu (munthu amene amayenda mozungulira dziko lapansi) wodziwika ndi—ndi kanema ya televizioni. Mawu aakulu a Mulungu, ndi Mzimu wa Mulungu ukutenga Mawu a Mulungu, kunyezimiritsa Yesu Khristu mmalo am'mwambamwamba kwa nkhosa Zake, kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Kodi Iye si wodabwitsa? Wodabwitsa! Mulungu akudalitseni inu.

276 Tsopano tiyeni ife tiyime kwa mphindi chabe. Kodi muli ndi winawake woti apereke mdalitso? Tsopano, kumbukirani, pa Khrisimasi, muzipembedza Ambuye Yesu. Muzimupembedza Iye mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake. Ndipo ngati ndingakhale wokonderedwa kwa inu (inu, abusa anu, mpingo wanu, kapena chirichonse), usiku sumakhala wamdima kwambiri, mvula siimagwa kwambiri.

277 Usiku wina (pali dona wayima pano) ndinali wotangwanika kwambiri, ndinatenga odwala ndi zinthu mpaka...Panali mayi wa zaka eyite chakuti amene anali atasokonezeka mutu, ndipo iye anali...iye ankaganiza zokhala ndi mwana kapena chinachake, iye anali atasokonezeka mutu. Ndipo Billy, kuchokera ku ofesi, anandiimbira ine, anati, "Adadi, kodi inu mungathe?"

278 Ine ndinati, "Sindingathe pakali pano. Pali anthu...Ine sinditha basi kuti ndichite zimenezo."

279 Iye anati, "Adadi, kodi mungapite kukapemphera? Ine ndiwauza iwo kuti mukupemphera."

280 Ine ndinati, "Inde." Ndipo pa nthawi yomweyo iye anakhalanso bwinobwino. Iye anagona tulo, anadzuka ali bwinobwino; anadya chakudya chamadzulo, nkhuku yathunthu, akuganiza bwinobwino. Munthuyo anaima pano akuchitira umboni za izo mphindi zingapo zapitazo.

281 M'bale Mack, ine ndinamuwona iye kuno kanthawi kapitako, penapake mu tchalitchi. Iye ali pano, mmodzi wa azibusa, m'busa wakuno. M'bale wokondedwa kwambiri, ndipo nthawizonse ndimamukonda Mbale Mack kuchokera pamene ndinayamba poyamba mu utumiki. Ndipo kenako ndinadzakumana naye...

282 Ndipo ine ndinali kutali uko mu British Columbia; ndipo kuti ndingokuwonetsani momwe Mulungu angagwiritsire ntchito zonse molondola. Ine ndinali nditakwera kale pa kavalo, ndipo ndinkabwerera ku chipululu kumene ndinatsogolera gulu lonse la Amwenye kwa Mulungu; ndipo onse anali atatembenuzidwa, ndipo anali atamulandira Yesu.

283 Ndipo mwa uneneri umene unamuuza mnyamata waku India amene anataya bulu wake, zaka ziwiri zapitazo, ndinamuuza iye kumene angakampeze iye, momwe kudzakhale kutalikira kwake, ndi kumene buluyo adzakhale atayima. Amayi ake akufa ndi matenda a mtima. Iye anachiritsidwa ndi kupulumutsidwa. Ndipo mnyamata uyu, akungobwera ndipo nkuziwona izo, ndipo podziwa kuti iye...kavalo wake anapezeka ndendende momwe iye anauzidwira, ndi chirichonse.

284 Palibe Mawu amodzi amene Ambuye anayankhulapo... Ndimufunsa aliyense wa inu, "Kodi Iye...inu munayamba mwamumvapo Iye akunena chirichonse, chimene Iye anandiuzapo ine kuti ndikuuzeni inu, koma chimene chinadzachitika ndendende basi?" Ngati uko nkulondola, nenani "Ameni." [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Mukuona? Mukuona? Ndendende, Izo sizinalepherepo konse nthawi imodzi.

285 Ndipo M'bale Mack anali atagona ali pafupi kufa, ndipo zinachitika kuti mkazi wake anamuimbira Billy...mkazi wa mwana wanga, ndipo anamuuza...anafunsa kumene ine

ndinali; dona wamng'ono wokondeka uja. . . mkazi wake. Ndipo iye. . . Ndipo mpongozi wanga anati, "Iye ali kumpoto kwa British Columbia pa ulendo wokasaka."

286 Ndipo mmawa umenewo, mwanjira ina, ine—ine—sindikanatha kukwera kavaloyo kuti ndizipita. Ndiyeno Billy anati, "Ndikukhulupirira kuti ndiimbenso kunyumba kamodzinso." Ndipo iye anapita kokaimbirako. Ndipo apa iwo anabwera akuthamanga, pamene Wachimwenye wamng'onoyo anayima pamenepo, wamng'onoyo. . . amene anali ndi bulu, ndipo anati, "M'bale Mack wagona pafupi kufa, ndipo akukuyitanani inu."

287 Ndipo ndinawuyamba, ndinapita mtchire ndipo ndinakagwada pansi. Ine ndinati, "Wokondedwa Mulungu, komwe kumusi, mailosi firii sauzande kutsidya kwa dzikoli, mdziko la dzuwa la Arizona, ku Tucson, kuli m'bale wanga, ndipo wagona ali pafupi kufa. Kodi mungamuthandize iye?"

288 Chinachake chinangoyankhula kwa ine, "Zonse ziri bwino."

289 Ndipo pamene ine ndinafika kwa M'bale Mack tsiku lina, kuti ndiyankhule ndi iye, ndipo ine ndinamufunsa iye, "Zinachitika ora lanji?" ilo linali ndendende ora lomwelo limene ife tinapita kukapemphera.

290 Oh, Iye. . . Kodi Iye si wodabwitsa! Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndine wokondwa kudziwa kuti ndimakhala mu Kupezeka kwa Mfumu.

291 Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano, ndipo m'bale wamng'ono wofunika ali pano, m'bale wamishonare, mzanga wa ine, membala wa Assemblies of God, m'bale wamng'ono wofunika pano. Ndimamutchula iye, "Creechy." Iye anayankhula zinthu zabwino chotere. M'bale Creech, ine ndimakutcha iwe chomwecho. Ine sindikudziwa choti ndinene, ndiwe m'bale wanga komanso wantchito mzanga mu zisautso za Yesu Khristu mu tsiku lotsiriza lino. Mulungu akudalitse iwe. Ndipo ine ndikuganiza M'bale Tony ananena kuti iwe ubalalitsa osonkhana pa nthawi ino, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu. Chabwino, bwera.

64-1221 Chifukwa Chimene Ankayenera Kukhala M'busa
Ramada Inn
Tucson, Arizona U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org